

MAFUNSO NDI MAYANKHO



Inu muli ndi chinachake choti mulalikirepo? [Winawake ati, “Ayi, bwana.”—Mkonzi.] Nanga bwanji M’bale Beeler apo? [“Ine sindikudziwa za iye.”] M’bale Beeler, kodi inu muli ndi uthenga wa usikuuno? [M’bale Beeler ati, “Ayi, bwana.”] I—ine ndangosasa mawu pang’ono. Ine ndinali nawo ena—mafunso ena panobe. Ngati iwo sati. . . Ngati mmodzi wa abale awa angati atenge ndi kulalikira, ine ndikanakhala wokondwa.

Tsopano, musati mutengeke. Izi si izo. . . Izi ndi nsalu zina chabe za pemphero zikupita ku Afrika. Zonse izi ndi zoti zikadulidwe kukhala nsalu za pemphero, ndipo iwo amafuna kuti ine ndizipempherere izo kuno usikuuno, kuwonjezera maenevelopu ena odzaza. Ndipo ine ndimaganiza kuti ife tingozipereka zonse izi k—kwa Ambuye. Zonse izi ndi zoti zikadulidwe kuti zipite ine ndisanapite ku Afrika. Tsopano, inu mukudziwa kuti ndi nsalu zingati za pemphero iyo iti ikapange pamene ziti zikakhale pafupi chidutswa cha kukula kwake chonchi chimodzi, zikwi za izo. M’bale Fred anabweretsa seveni handiredi tsiku lina mu envelopu yaing’ono pafupi monga choncho. Ndipo inu mukhoza kulingalira chomwe iyi—kuti iyi ikapanga zochuluka bwanji. Chotero ndife. . . Basi pang’ono pokha, bwanji, ife tipempherera pa iyo.

² Tsopano, ine ndangosasa mawu pang’ono, koma ine ndinanena kuti ndibwerera kuti ndidzayankhe ena a awa—mafunso awa mwakukhoza komwe ine ndingathe. Ndipo tsopano, nthawizonse, pamene zitsitsimutso izi zimabwera motsatirapo, izo zimayambitsa kugwedeza pang’ono. Ndipo ine ndikufuna—ndimaganiza mwinamwake izi zingathandizepo ndi mpingowu usikuuno, inu mukudziwa, chifukwa nthawizina chinachake mwina chikhoza kukhala chitanenedwapo chomwe mpingo sunachimvetse icho. Ndipo iwo akupatsani inu mwayi woti mulembe funso lanulo tsopano. Ine ndikupatsani inu omwe ine ndiri nawo; ndiyeno, ngati inu muli ndi chirichonse chonga iwo, inu simusowa kuti mulilembe ilo.

Ndiyeno limodzi la iwo ndi ili: **Chonde tafotokozani Aroma 7:25.**

Lina lotsatira: **Inu munati munthu akhoza kumakhala pafupi kwambiri ndi Mulungu mwakuti iye sangachimwe.**

Kodi ndi maonekedwe anji titi tidzakhale nawo mu chiukitsiro?

M’bale Branham, kodi munthu azichita chiani pamene iye watsatira malangizo onse omwe inu mwaphunzitsa; ndiyeno, iwe ungalandire chotani Mzimu Woyera?

Chonde tafotokozani Aheberi 6:4 ndipo mufanizitse apo ndi Aheberi 10:26.

Ndi: Zimatanthauza chiani kukonzedweratu asanaikidwe maziko a dziko; ndipo ndi pati mu Baibulo pomwe inu mungazipeze zonga izo?

- 3 Ndipo Mulongo Mc . . . Ayi, i—ilo ndi pempho la pemphero.
- 4 Tsopano, awo ndi mafunso athu omwe ife tiri nawo kwa usikuuno. Ngati inu muli nalo lina pomwe ife tikungoyambapo pang’ono apa, chabwino, inu mulibweretse ilo, ndipo ife basi tingoyesera . . . Tsopano, ngati pali fuso lirilonse mmalingaliro a mpingo lokhudza chirichose l—lomwe ife tiri nalo, bwanji ife talinga k—kuti tikhale okhoza k—kukuthandizani inu mwakukhoza momwe ife tikudziwira. Mwaona?
- 5 Ndipo ine ndikufuna inu kuti muzikumbukira nthawizonse kuti zomwe ine ndikuzinena pano, ine sindikunena kuti ndizo Choonadi motsindika ndi chirichose. Ndi mwakupambana komwe ine ndikudziwa kuti chiri Choonadi chotsimikizika cha izo. I—ine ndikhoza kukhala ndikulakwitsa chimodzimodzi monga wachivundi wina aliyense, koma ine ndikungoti, M’bale Jackson—ndikungoyesera kufotokoza izo momwe ine ndikuganzira kuti ndi kulondola (inu mukuona?), momwe ine ndikuziwonera izo, M’bale Mike, mu Baibulo, basi. . . . Ndipo powerenga zinthu izi, ine sikuti ndimangozitunga izo kuchokera pa malo amodzi. I—ine ndimapita mmbuyo ndi kukazibweretsa izo kuchokera ku Genesis, ndi kuzibweretsa izo kudutsa mpaka ku Chivumbulutso, molunjika kumene kudutsa mu Baibulo.
- 6 Ndiyeno, inu mukhoza kuzibweretsa—ngakhale kulidutsitsa mphunzirolo. Koma, ngati izo sizinagwirizane ndi onse a Iwo mmenemo, Malemba onsewo, ndiye izo zikanakhala zolakwika mulimonse. Ngati inu mukanazibweretsa izo mulimonse, izo ziyenera k—izo ziyenera kumagwirizana ndi Malemba ena onsewo. Inu mukuona? Ndipo Malemba onse amalumikizana limodzi ngati Iwo aikidwa molondola palimodzi, ngati. . . Ziri ngati basi zidutswa zopanga china chachikulu. Ndipo ine sindikuthauza. . . Ngati ine ndikunena izo molakwitsa, ndiye Mulungu andikhululukire ine. Lemba ndi chinachake chofanizidwa ndi zidutswa zopanga chithunzi. Mukuona? Izo. . . Izo ndi zophwasulidwa ndi kungosakanizidwa mu bokosi, ndipo zimatengera Mzimu Woyera kuti ziyike izo palimodzi. Mukuona? N—ndipo ife sitingakhoze kuzichita izo. Tsopano, palibe kutanthauzira 969 kosiya kwa Iwo, chifukwa Baibulo linanena kuti Lemba ndi lopanda kumasulira kwa mseri. Zimangokhala basi momwe Iwo analembedwera. Ife timangowakhulupirira Iwo k. . . (Zikomo inu, M’bale Pat.) Ife. . . Iwo ndi basi momwe Iwo—Iwo analembedwera mu Baibulo; ndi momwe ife timayenera kuti tizitunga Iwo, monga choncho. Chotero ngati ife tiyesera kuti tiziwapanga Iwo

kunena chinachake apa, chabwino, Iwo samanena chinthu chomwecho cha kuno. Mwaona, ngati i—ngati ife tiika. . . Inu muyenera kuti muzilipangitsa Lemba kuti lizidziyankha Lokha apa, lizidziyankha lokha apa. Lizidziyankha lokha apa, basi lirilonse lizipita pa malo Ake omwe kuti tiwapange Iwo onse kulumikizana palimodzi.

⁷ Ndipo tsopano, ine ndimaganiza mwinamwake. . . Ine ndimati ndiyankhule ndipo ine ndimati ndikanatero usikuuno, *Ife Taiwona Nyenyezi Yake Kummawa, ndipo Tabwera kuti Tidzampembedze Iye*; koma ine ndangokhala kuti ndiribe mawu okwanira, ndiyeno, kuti ndichite izo. Ine ndinatenthedwa pano usiku ndipo ndinatuluka. Ndipo ine ndinali nditatenthedwa kwambiri pamene ine ndinakalowa mu galimoto, ine ndinangoitenthetsa iyo kwathunthu. Ine ndinatsitsa zenera pansu ndi kumapita kunyumba. Chabwino i—ine ndikuganiza ilo linali Lachinayi kapena Lachisanu usiku. Usiku wotsatira womwe, ine ndinayamba kukhala—tsiku—ine ndinayamba kusasa mawu pang’ono, kukhala ngati. . . O, ndi. . . Ine sindiri—sindiri kudwala, ndiribe litsipi, ndiribe matenda, ndiribe malungo; koma zangokhala ngati—kung’ambika pang’ono pammero pako basi chifukwa cha kuyankhula n—ndi kuvulazidwa chifukwa cholalikira zolimba, ndiyeno—ndiyeno panazizidwa. Koma pa—pakhala bwino bwino mu tsiku lina kapena awiri, mwinamwake pofika Lamlungu. Ine ndikhoza kungobwera kuti ndidzamuthandize M’bale kachiwiri. Iye atathana ndi kulalikira kwake, ine ndifufuza kuti ndiwone kuti nchianinso chatsalira.

⁸ N—ndiyeno ine ndikufuna mpingo wonse kuti ulandire Mzimu Woyera. Tsopano, mpongozi wanga wamkazi wakhala apa. Osati chifukwa kuti ndi mpongozi wanga wamkazi, osati chifukwa kuti iye ali pano, iye ndi mmodzi wa asungwana abwino kwambiri omwe ine ndikuwadziwa iwo; iye ndi msungwana wabwino zedi, Loyce. Ndipo iye wadutsa kuchokera mu zinthu zazikulu kuchokera momwe iye anakulira, komwe iye anachokera ku banja lomwe silinali kupembedza Mulungu ndi zina zotero. Ine ndimamumvera chisoni mwanayo, kukhala atakuzidwa moteromo. Ndipo tsopano, iye akufuna Mzimu Woyera, ndipo wasala mpaka iye sakukhoza ngakhale kuima, kusala ndi kupempherera pofuna Mzimu Woyera.

⁹ Mlongo wanga, Dolores, iye anati, “Bill, ine basi. . . pamene mpingo unali—mphamvu zinali mu mpingo,” iye anati, “Ine ndinangomverera ngati kuti ndikanakhoza kuwulukapo. Ndiyeno, pamene aliyense—Mzimu woyera unayamba kugwera pa anthu,” anati, “Ine ndinangokhala apo ndipo ndimayang’ana pozungulira.” Mukuona? Chabwino, onani, ndipo funso limenelo liri muno pano usikuuno, pa zimenezo. Chotero ine ndinaganiza mwinamwake izo zikanakhoza kuuthandiza mpingo k—kuti ulandire. Ndipo tsopano, ine sindikufuna kuti ndidzatenge

msonkhano wa pemphero wa Lachitatu ndi kudzalowerera mu chinachake chonga izo, koma i—ine ndikufuna kuti ndikhale wotsimikiza kuti mpingo ukumvetsa bwino bwino zinthu izi (inu mukuona), tisanati. . .

¹⁰ Ndipo ine ndinali kungoyankhula kwa adotolo kuno Lamlungu, anabwerera kumbuyo kwa kachisiyu kuno k—kumbuyo kuno kuseri kwa tchalitchi. Iwo ndi dotolo wazamankhwalu. Iwo anali atayendetsa njira yonse kuchokera (kodi likulu la Assembly of God liri kuti pakali pano? Mu. . .) ku Springfield, Missouri, kudzakhala nawo pa msonkhano.

Ndipo iye anati, “M’bale Branham. . .” (Tsopano uyo ndi wochokera ku likulu la Assemblies. Ndipo iye anati, “Moyo wanga wonse ndakhala ndikudabwa pa izo.” Anati, “Iyo ndi nthawi yoyamba yomwe ine ndinayamba ndakhazikika pa izo mu moyo wanga.” Iye anati. . .Anakomana nane ine kumbuyo uko mu chipinda, tinakhala, dotolo wazamankhwalu.

¹¹ N—ndipo chotero, M’bale Mercer ndi M’bale Gene Goad kumbuyo uko ali ndi marekoda. . .Pakali pano, M’bale Mercer anati anapeza chopambana kuchokera mu msonkhano p—pomwe ife tinafotokoza k—kuti pamene Mzimu Woyera uja unadza mu msonkhano n—ndi kudzadzigawa Wokha apo, ndi Mulungu akudzigawaniza Yekha pakati pa anthu Ake. . . Chabwino, izo basi ndi zomwe Iwo umachita. Ndiyeno, pamene anthu a Mulungu ayamba kusonkhananso palimodzi, pamakhala chiyanjano, pamakhala mphamvu. Mukuona? Ndipo paliponse pamene anthu a Mulungu abwera palimodzi kwathunthu, ine ndikukhulupirira chiukitsiro chidzachtika apo ndiye. Padzakhala nthawi ya mkwatulo pamene Mzimu Woyera udzayamba kuwasonkhanitsa iwo. I—iwo adzakhala apang’ono, ndithudi, koma kudzakhala kuli kusonkhana kwakukululu.

¹² Tsopano, nsalu za mapemphero izi zimatumizidwa, Liwu la Machiritso. . .Ine pomwepo mwamsanga, koyamba kwa chaka, ngati Ambuye alola, i—ine ndikupita ku Kingston, Jamaica, kukalowa mu Haiti, ndipo kuchokera uko. . .P—purezidenti waku Haiti wanditumizira ine kuitana, n—ndi asirikali onse mwa chitetezero. Iwo ali ndi kuukira kumeneko. Ndipo chomwe izo ziri, iye akufuna kuti ife tibwere ndi mtundu uwu wa utumiki, umene iye anaumva ali uko mu—ku San Juan chaka chatha pamene ife tinali uko. Iye akuti iye akuganiza kuti icho ndi chinthu chokha chomwe chingalipulumutse dziko lake. Mukuona?

¹³ Tsopano, ngati ine ndiri ndi mzanga wa Chikatolika atakhala apa, ine sindikunena izi k—kuti ndikunyozeni inu kapena chirichonse; ine sindikutanthauza izo mwa njira imeneyo. Koma mpingo wa Katolika ukuyesera kuti ulande Haiti (mukuona?); ndipo chinthu chokha chomwe chiti chimupulumutse iye, chikhala chirichi chitsitsimutso cha

Chiprotestanti, chogwedeza pakali pano. Mukuona? Ndipo izo ndi zabwino kwenikweni, ndipo ine ndikuyamikira izo. Ndipo kotero ine ndinamuuzza iye, mu sabata ya Khirisimasi ndi masiku pang'ono otsatirawa tsopano, nkucha, timka mokhala ngati kusala ndi kupemphera, ndi kuwona njira yomwe Ambuye ati atitsogolere ife.

14 Ndiye South Amereka...Ndiyeno, ine ndikumverera kutsogozedwa motsimikizika kuti ndipite ku—Norway. Ine ndikutsogozedwa kwenikweni basi kuti ndipite ku Norway chaka chino, ndipo kenako, Afrika nakonso. Ndipo izi zakhala ziri—zikadulidwa mu timariboni tating'ono ndi kukatumizidwa ku Afrika patsogolo pa msonkhano. Ndiko kuchuluka kwa anthu... Inu mukhoza kukhala ndi lingaliro wamba kuchuluka kwa anthu omwe akuitanitsa nsalu za pemphero tsopano pamene iwo amva kuti iwe ukubwera uko (mwaona?), basi—akungopeza momwe angatifikire kachiwiri. Kotero izi ndi nsalu zazing'ono zomwe zadulidwa nazonso ndipo zakonzeka kuti zitumizidwe uko—kwa anthu osiyana.

15 Chotero limodzi ndi Mpingo waukulu uwu wa Mulungu Wamoyo, tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha tsopano. Ndipo aliyense wa inu mwa njira yanu yomwe, zipempherani kuti Mulungu adzozze zovala izi. Tsopano, poyamba ine ndikubwereza Lemba lakuti, “Kuchokera ku thupi la Paulo iwo anatenga mipango kapena tizovala, ndipo anakaziika izo pa odwala, ndipo mizimu yoipa inatuluka mwa anthuwo, ndi zosautsa; ndipo iwo anali kuchiritsidwa.”

16 Ambuye, pa desiki yaing'ono iyi yomwe yakhala ili apa kwa zaka zonse izi, ndi momwe Inu mwakhala mukutidalitsira ife mochuluka kwambiri, ndipo—Uthenga mowirikiza wakhala ukupita konse konse uku, ndi...Ngati desiki yaing'ono iyi ikadakhala kokha ndi maso kapena ikadamayankhula, iyo ikadakhocha kunena za zozizwitsa zazikulu mazana zomwe zakhala zikuchitidwa patsogolo pa ilo pomwepo: opuwala, olumala, akhungu, ogwidwa ndi khansala. Ndipo mphamvu za Mulungu Wamoyo zakhala zikudziwitsidwa mu nyumba yaing'ono iyi. Ndipo Atate Mulungu, ife tikungokuthokozani Inu chifukwa cha zinthu zonse izi.

17 Ndipo tsopano, mpingo wasonkhana limodzi usikuuno kuti ukupembedzeni Inu. Ife tabwera ku—kuti tidzayankhe mafunso omwe afunsidwa. Ndi kudzipereka ndi mitima ya anthu kuti zinthu izi zimawadodometsa iwo mmalingaliro awo. Ndipo Ambuye, ife tiri kuzindikira, kuti ngati chirichonse chiri kutidodometsa ife, ife sitingakhoze konse kukhala nacho chikhulupiriro, utali wonse pamene pali funso. Chotero ife sitirikufuna mafunso aliwonse.

18 Ambuye, ife tikuwona kufunikira kwa ubatizo wa Mzimu Woyera pakati pa anthu athu ndi pakati pa mpingo uno. Ndipo

i—ife sitikufuna mafunso aliwonse mu malingaliro awo. Ife tikufuna izo zonse ziyeresedwepo, chotero kuti iwo adziwe chomwe iwo uli pamene Iwo uzibwera, ndi kudziwa kuti Iwo ndi wa iwo.

¹⁹ Ndiyeno, kudutsa nyanja, kutali uko mu nkhalango za mdima izo komwe ng'oma zikuwombodwa, ndipo akhate ali paliponse mu—pansi pa mitengo, ndipo ntchentche zikuwomba, n—ndipo miyendo yawo itadukapo ndi makutu awo atadyedwapo ndipo nkhope zawo zitadyeka, khate. Fungo, Ambuye, mpaka iwe sungakhoze konse kubwera pafupi mdadada wa mu mzinda kwa iwo. Ndipo ana aang'ono osauka opanda chakudya, opanda zovala...Ndipo iwo amandikonda ine, Ambuye. Ndipo i—iwo awukhulupirira utumikiwu, Mphamvu ya Mulungu Wamoyo itachiza kale ochulukwa kwambiri a iwo. Ndipo ine sindinakhalepo ndi mpumulo mu mzimu wanga kuyambira tsiku lomwe ine ndinachokako ku Afrika, podziwa kuti anthu osauka awo, okanidwa ali mu chikhalidwe choipa icho uko, ndipo akukhala mu zikhaldidwe zamatsenga. Ndipo asing'anga, ali ndi mafupa a anthu akuwamenyetsa iwo mzala zake, ndi kumaitanira pa mizimu yoipa, ndipo o, malo—akewo, ndiyeno kuganiza, kuno mu Amereka, mipingo yokondeka ndi malo aakulu. Ndipo, Mulungu, ndi podziwa kuti anthu osauka awo ali osowa kwambiri, ndinawawona iwo akubwera ku msonkhano, atakhala pamwamba pa mzache, ndipo ambiri a iwo akufa atagona pamenepo, akungoyesera kuti amve mawu pang'ono kuchokera kwa winawake yemwe iwo amati kuti amakudziwani Inu. Mitima yawo yayamba kukwera, Ambuye, pakuti Uthenga ndi makalata akusesa ku Afrika konse tsopano. Moto, zikuwoneka ngati, ukuyamba kuyatsidwa kachiwiri.

²⁰ Ndipo mpingo Wanu waukuluwo uko, umene unali mpingo wamphamvu, unasweka mu zidutswa, o Mulungu, ndi kulekanitsidwa ena mu gawo la mwachizolowezi, n—ndipo enawo akuyeserabe kuti agwiritse ku Choonadi ndi Mzimu. Ndipo tsopano, zikwi akutumizira kuno tsopano; iwo akufuna nsalu za pemphero mofulumira zomwe—ine ndapempherera pa izo. Mu maenvelopu aang'ono awa pano muli zopemphera za pemphero zathu, timaphukusi tating'ano tomwe tikupita kwa osowa. O, Mulungu wa Kumwamba yemwe munapanga miyamba ndi dziko lapansi, ine ndikukupemphani inu, Ambuye, mu Dzina la Yesu kuti Inu muyeretse ulusi uliwonse wa nsalu iyi. Ndipo mulole Mzimu Wanu Woyera upite ndi ulusi uliwonse wa iyo, Ambuye. Ndipo pamene ziti zikaikidwe pa odwala ndi osautsika, mulole mizimu yoipa ikawachokere iwo.

²¹ Kuganiza mmbuyo mu nkhalango izo komwe zinthu izi ziti zipiteko, zambiri za izo, komwe iwo ali—mpaka kumampembedza mdierekezi. Ine ndikukupemphera, Mulungu, kuti asakakhale ndi malo amodzi oti akaimpepo, kuti iye

akachoke ku midziyo, ndipo anthu akabweretsedwe ku chidziwitso cha Ambuye Yesu. Perekani izi, Ambuye. Mulole matenda awo akachiritsidwe, mavuto awo akakonzedwe, ndipo miyoyo yawo ikapulumsidwe, ndipo Mphamvu ya Mulungu ikakhale ndi uyambiriro. Perekani izi, Atate. Ife tikutumiza ulusi uliwonse wa nsalu izi ngati chinthu chimodzi. Malawi ambiri aang’ono a moto ali pano usikuuno, Ambuye, ndipo palimodzi ife tikutumiza mapemphero athu kwa Inu mmalo mwa izi, kuti munthu aliyense akachiritsidwe yemwe zikaikidwa pa iwo. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²² Tsopano, kodi inu mukukhoza kundimva ine kumbuyo, mwabwino kwambiri kumbuyo uko tsopano usikuuno? Izo nzabwino. Ine ndikuganiza ife tidzakhala okondwa kwambiri ife tikadzapeza kachisi wina pano, chifukwa zinthu zazing’ono izi zagwira pansizi, zimakudula mawu ako ndipo i—iwe sungakhoze kuzimva izo nkomwe.

²³ Tsopano, ine ndikuzindikira apanso usikuuno, i—ine ndikuyandikira malo. . . M’bale Wood, ine ndisanati ndiiwale izo, ine ndiri nao mpango uja. Kodi inu simunandipatse ine mpango wa winawake? Kapena kodi uyo anali inu? Winawake anandipatsa ine mpango kuti ndiziyika pa thumba langa ndi kumavala; ndipo ine ndakhala nawo iwo chiyambireni pamenepo, mu nthawi ya msonkhano. Ine sindikudziwa yemwe iye ali. Ine ndimaganiza kuti munali inu munati, “Muzivala uwu mthumba mwanu mmalo mwa winawake.” Wina. . . [M’bale Neville afotokoza za mpango kwa M’bale Branham—Mkonzi.] Kodi izo zinali choncho? M’bale Jackson, kodi inu munali ndi mpango wa winawake? Ndi uwu iwowo. Chabwino. Uwu. . . Chabwino, uwu ukhala uli pomwe pano, M’bale Jackson, ngati inu mukuufuna iwo. Ndipo tsopano, ine ndikudziwa winawake anawupereka iwo kwa ine, anati, “Ziuvalani iwo mthumba mwanu.” Ndiyeno, ine ndinawuika iwo mu chikhoto changa ndipo ndinaiwala za iwo.

²⁴ Tsopano, kwa. . . Tsopano, ngati Ambuye alola, ndipo liwu langa likakhala bwino bwino, mwina Lamlungu mmawa kapena Lamlungu usiku, lina, Ambuye akalola, ine ndikufuna kuti ndidzayankhule pa uthenga wa Khristimasi womwe ine ndiri nawo kwa inu: *Ch—Chizindikiro Chosalephera*. Inu mukuona? Ine ndikadali. . . Ine ndinachikhudza icho Lamlungu mmawa, ndiyeno, chinachake chinagunda moto mu mtima mwanga. Ndipo ine ndinangokhala ndiri patali ndi uthengawo kuti ndichitenge icho kachiwiri. Chotero i—ine ndikufuna kuti ndidzatenge icho Lamlungu mmawa, Ambuye akalola, kapena Lamlungu usiku, wina. Chotero M’bale Neville ndi ine tidzakhala limodzi pa nthawi imeneyo.

²⁵ Tsopano, monga M’bale Neville wanenera, ndipo chomwechonso ine ndikufuna kuti ndimuthokoze aliyense wa inu chifukwa cha zikumbutso za Khristimasi, makadi

anu. M'bale ndi Mlongo Spencer, ine ndalandira yanu. Ndi onse osiyana pano omwe munanditumizira ine makadi anu, konsekonse, ine ndikuwayamikira iwo ndi mphatso ndi zinthu zomwe inu munatumiza. Ife ndithudi tikuyamikira izo. Ku—kuchokera kwa mkazi wanga, ndi ine, ndi—ife—ndi ana, ife tikukuthokozani inu. Ife tikadafuna tikanakhala okhoza kutumiza mphatso ya Khristimasi kwa aliyense, koma izo ndithudi zingakhale chinthu chovuta kwa mlaliki kuti achichite, sichoncho izo? Chabwino, mwinamwake pafupifupi kwa ochuluka omwe ukanati uzipitako, ine sindikanakhoza basi kuti ndichite izo. Inu mukuona? Ine basi...Koma ine ndimakhumba ndikanangowapezera ana, mmodzi aliyenseyo, chinachake. Ine ndithudi ndikanakhumba kuchita izo, koma izo siziri basi... Utumiki uwu sungakhoze kuchita izo. Mukuona? Pali basi zochuluka kwambiri zoti upite ukagule. Koma ndife tonse, ine ndikutsimikiza, inemwini ndi ena nawonso, kuti ife tikuyamikira gulu lathu. Chimodzi mwa zinthu zazikulu kwambiri zomwe ine ndikuganiza kuti inu mwachita, ndi chikondi chanu ndi chikhulupiriro chanu chosafa chimene inu mwachiyika mwa ine ngati m—mmodzi mwa abusa anu pano, ndi—chaka chino.

²⁶ M'bale Neville, izo ziri za kwa inu aponso, m'bale wanga wokonedwa. Ndi mzimu wabwino umene M'bale Neville nthawizonse wausonyeza, monga, “Bwerani komwe kuno, M'bale Branham; guwa ndi ili, litengeni ilo kumene. Mulungu adalitsike, ine ndimakonda kukhala pansu ndi kumamvetsera.” Ndipo i—ine ndimazikonda izo. I—ine ndimangokonda kachitidwe kodzichepetsa, kosadzikonda komwe M'bale Neville ali nako.

²⁷ Ndipo nonse inu ndi chikhulupiriro, ndi basi...Chinthu chimodzi chomwe inu mungandichitire nacho chifundo ine, ndi kundipempherera ine. Tsopano, ine ndikhala ndiri ndi mulu wa misonkhano ya apa ndi apo tisanayambe kuyenda kwakukulu. Tsopano, i—izo ziyikidwa pozungulira, ine ndikuganiza, uko cha ku Glasgow, Kentucky, ine ndidzakakhala ndi usiku. Mwinamwake Campbellsville, Kentucky, ine ndidzakakhala ndi usiku. N—ndipo cha ku malo ena uko mu Kentucky, Willow Shade, ine ndikukhulupirira nkomwe kuli, ine ndikakhala ndi usiku. B...Basi mongotsatira monga, ine ndidzakudziwitsani inu mofulumira basi tikadzazikonza izo, za misonkhano yomwe ikudzapo, yomwe iti idzakhale misonkhano yaing'ono ya apa ndi apo tsopano, mpaka ine ndidzabwererenso ku mundawu kachiwiri.

²⁸ Koma ine ndinadzipereka ndekha mwatsopano ndi mwabwino usiku wina kwa Mulungu. Ndipo mwa kuthandiza kwa Mulungu ndi mwa chisomo cha Mulungu ine ndikutanthauza kukhala ndiri mu goli mpaka ine ndidzafe. Mukuona? Ine ndinachita izo pafupi zaka sate zapitazo.

Ndipo ine ndakhala ndiri umo...Koma ine ndimatopa kwambiri nthawizina, ine ndimafika podzipitirira ndekha. Ine ndimangofika pamalo pomwe ine sindingakhoze basi kupita patsogolo paliponse. Mwaona, inu nonse mwina mumangoziwona izo pomwe pano. I—inu simumazindikira basi kuti ndi chiani kumtunda uko, ndi kutali uko, ndi cha kuno. N—ndipo osati nkomwe kuchokera ku umodzi—osati kuchokera ku mzinda umodzi, ayi; boma limodzi, ayi; osati kuchokera ku United States; koma mdziko (mukuona?), kuzungulira mdziko. Mukuona? Ndipo a—awo ndi ochuluka, ine ndikulingalira, akulembera kuno usikuuno, ine ndakumana nawo kapena ndalemberana nawo, osati mwa zikwi, koma anthu mamilioni. Mukuona? Ndipo inu mukhoza kungokhala odabwitsidwa kuti ndi angati a iwo omwe ali odwala. Mukuona? Ndipo iwo akuitana; ndipo izo zimapanga chipsyinjo chachikulu.

²⁹ Chotero ine ndikuyamikira mapemphero anu onse. Ndipo mwa kuthandiza kwa Mulungu ndi chisomo, Khrisimasi Yachisangalalo kwambiri ikhale kwa aliyense wa inu. Zikumbukirani zonena zanga, izi si Santa Claus, izi ndi za Yesu. Inu mukuona? *Khristimasi* imatanthauza “Khristu.” Ndipo ife tinali kuyendetsa usiku watha, tikuwasonyeza ana manyumba onse atakongoletsedwa ndi chirichonse, chomwe chiri chabwino kwambiri. Koma ine ndinaganiza, ngati ine ndikanakhala nacho konse—chirichonse pa nyumba yanga, chomwe ine ndikanafuna kuti ndilembe konse, chikanakhala cholembedwa ndi magetsi: *Ndikudalira kuti Khristu Akhalamo Mu Khristimasi Yanu*. Ndiko kulondola. Kumuyikanso Khristu mu Khristimasi momwe.

³⁰ Tsopano, Atate Mulungu, ife tikuyandikira mafunso tsopano. Modzipereka kwambiri, mbiri ife tikubwera. Ndipo—anthu ofunikira awa, Ambuye, ayika mafunso awa ndi—omwe ali pa mitima yawo, ndi mwinamwake ochuluka ena ali mu nyumbayi; ndipo iwo akufuna kuti adziwe basi choti achite. Ndipo Atate, i—ine ndi choloweza mmalo chosauka kwambiri cha Inu, koma ine ndikupemphera kuti Inu mundithandiza ine kuti ndiwadziwe Mawu Anu, kuti Iwo abweretse gawo lokhutitsa kwa funso lirilonse. Izi ndiye ife tikuzisiya mmanja Mwanu, ndipo mu Dzina Lanu ife tikupempha izi. Amenii.

³¹ Tsopano, funso la M’bale Pat pano ndi lina, labwino kwambiri mbiri. Ine mwina ndikhoza kungoyambira pa ilo, M’bale Pat. Tsopano, ngati wina aliyense wa inu ali nalo funso, inu ingolilembani ilo ndi kuliyika ilo apa, k—kapena M’bale Pat akubweretserani inu chidutswa cha pepala ngati inu mulibe chidutswa cha pepala; kapena ine ndikhala wokondwa basi kuti ndichite chopambana chomwe ine ndingathe kuti ndiziyankhe izo.

Tsopano, ili ndi funso ndithu, M’bale Pat. Izi zikumveka ngati kuyankhula mosangalatsa, koma ndi funso.

101. Kodi ilikuti mizimu ija tsopano yomwe inapita kukalowa mwa nkhumba? Ilikuti mizimu yomwe inapita ndi kukalowa mu gulu la nkhumba tsiku lija pamene Yesu anaitulutsa kuchokera mwa wamisala?

³² Chabwino, M'bale Pat, mwakukhoza kwa kudziwa kwanga. . . Tsopano, ife tikuyamba pa zaziwanda poti tiyambire. Tsopano, zaziwanda ndi chinthu chachikulu. (Tsopano, ena a inu muziyang'ana pa koloko ndipo musandisiye ine kuti ndizipita motalika kwambiri pa funso limodzi.) Koma mphamvu za ziwanda izo, mizimu imeneyo inali mwa munthu wotchedwa Legio poyamba. Si kulondola uko? Ndi chifukwa dzina lake anali Legio, chifukwa *Legio* mu Chihebri amatanthauza “ambiri.” Mukuona? Zinalipo zambiri za izo.

³³ Ndipo mizimu iyo yomwe inali mwa munthu wokondeka uja inali kumuyendetsa iye mwa misala. Ndipo ngati aliyense anayamba wamuwonapo munthu wamisala kapena anachitapo ndi iwo, iwo ali mochulukitsa kambiri m—m—mphamvu zawo, chifukwa iwo amagwidwa kwambiri ndi mdierekezi. Ngati inu munayamba mwakhalapo komwe—munthu wasokonezeka malingaliro, o, izo zimatengera anthu abwino angapo kuti awagwire iwo. Ndipo iwo amakhala pawiri kapena patatu mphamvu zawo.

³⁴ Tsopano, pamene munthu ali wolumala ndipo Mzimu Woyera ukawagwira iwo, ngati mdierekezi ali ndi mphamvu yochuluka chomwecho yoti nkumupangitsa munthu kukhala katatu kapena kanai mphamvu zake zaumunthu, ndi mphamvu zochuluka bwanji zomwe Mulungu angakhoze kuziika mwa munthu? Mukuona? Ndi zomwe zimabwera pa iye kudzamupangitsa iye kuti aziyenda mu mphamvu ya Mulungu, pomwe iye wakhala ali wolumala kwa zaka. Mafupa ake amawongoka; ndipo manja ake amawongoka; iye amayenda, ndi ngati mnyamata watsopano, chifukwa mphamvu ya Mzimu Woyera ili pa iye.

³⁵ Tsopano, iyi inali yoipa kwambiri mpaka iwo ankamukulunga munthuyo mu unyolo, ndipo iye ankakhoza kuwudula iwo. Ndipo iwo anati iye amawumwetula iwo pakati. Ndipo uko—kunalibe kanthu komwe kakanamumanga iye. Iye anali kwenikweni mu vuto loipa kwenikweni, chifukwa iye anali ndi chikhamu cha ziwanda mwa iye. Ndiyeno, pamene iye. . . Yesu anawolokera uko ndipo anabwera mu Gadara ndipo anauyamba kupita cha ku manda. . . Ndipo iye anali woipa kwambiri, osati munthuyo (mwaona?), munthuyo anali wabwino bwino.

³⁶ Si munthuyo. Pamene inu mumuwona munthu monga chomwecho, musati muziganiza konse kuti ndi munthuyo; ndi mdierekezi yemwe ali mwa munthuyo.

Tsopano, wamisala uja pa nsanja usiku uja, ankafuna kuti andiphe ine, uko mu Oregon. Munthu uja, p—pamene

iyе anabwera kwa ine, mmalo moti iye atandilavulira ine mu nkhope yanga ndipo ananditcha ine “njoka mu udzu” pamaso pa pafupifupi anthu zikwi khumi, chabwino, izo sizinali kuti, uyo sanali munthuyo. Iye ndi munthu yemwe amadya, amamwa, amagona, mwinamwake ali ndi banja, ndipo amakonda, n—ndi basi monga momwe ine ndiriri kapena inu muliri. Koma anali mdierekezi uja mwa iye yemwe anali kuchita izo. Mukuona?

³⁷ Ndipo inu simungakhoze konse kumutulutsa mdierekezi ndi cholinga cholakwika. Izo zimatengera chikondi kuti muchite izo. Ndipo chikondi ndi mphamvu yokankha kwambiri yomwe ilipo mu dziko. Tsopano, ngati inu mungazindikire, mdierekezi nthawizonse amada. Udani ndi wa mdierekezi. Ndipo pamene anthu amuda winawake, kumbukirani, ndi mdierekezi woopsya kunyoza kapena kusakonda. Musati muzichita izo.

³⁸ Inu mukukumbukira izo—z... Yesu ananena mu ulaliki Wake kuti pamene inu mukupemphera, “Atate Athu Omwe muli Kumwamba,”... Ndipo pamene Iye anabwera mmusimo, Iye anati, “Ngati inu simungakhululuke kuchokera mu mtima mwanu munthu aliyense zolakwitsa zake, Atate anunso akumwamba sadzakukhululukirani inu zolakwitsa zanu.” Mukuona? Inu musati muzichita izo.

³⁹ Koma tsopano, pamene mdierekezi alenga mphamvu ya udani (mukuona?) kuti athamangire pa nsanja ndi kudzandipha ine, chomwe iye mwathupi, iye anali wokhoza kwambiri, kuchulukitsa nthawi zambiri zina... Iye akanakhoza kundinyamula ine mmwamba, mwinamwake, mwa zala zake ziwiri, atandigwira lamba monga chomwecho, chifukwa iye ankalemera 260 kapena 270; iye anali mwabwino wamtali kuposa mapazi sikisi ndi theka kapena mapazi seveni, munthu wamkulu kwambiri. Ndipo basi... Iye anali atamumenya kumene mlaliki uko ku msewu ndi chibakera chake, anaswa phewa lake ndi chibwano, ndipo anamuvulaza iye, ndipo anakamuika iye ku chipatala. Iye ankangodana ndi azilaliki. Ndiyeno, iye anangothamangira uko apo kuti adzandiphe ine. Mukuona?

⁴⁰ Tsopano, mwa munthu ameneyo munali ina ya mizimu iyi yomwe inatulutsidwa kuchokera mwa nkumba ku Gadara. Ena a anthu osauka awo ali kuno kwa azamisala, akumenyetsa mitu yawo pa zitsulo zotetedzera, ndende. Kumbukirani, ziwanda sizimafa konse. Ziwanda nthawizonse zimakhala moyo, koma idzakhhalapo nthawi yomwe ziwanda zidzayenera kuti zidzafe. Izo zidzakhala zitatheratu kwathunthu. Koma tsopano, izo ziri moyo, ndipo izo zagwira ntchito kuchokera ku kam’badwo kupita ku kam’badwo pa anthu okhalapo. Zina za izo ziri mwa mawonekedwe a khansara; zina ziri mu mawonekedwe a khunyu; zina ziri mu mawonekedwe a chifuwa. Izo zimalowa mu mnofu, koma mwakuwoneka, izo ziri zopanda mphamvu mpaka izo zitalowa mwa munthu. Izo zimayenera kugwira ntchito

kupyolera mwa munthu, chimene chikutibweretsa ku lingaliro lina, kuti Mzimu Woyera uli—umaphimba dziko lapansi, koma Iwo uli pafupi wopanda mphamvu mpaka Iwo utalowa mwa iwe ndi mwa ine.

⁴¹ Mulungu akudalira pa inu ndi ine. Mukuona? Mzimu Woyera. . . Dziko lapansi liri lodzaza ndi Mzimu wa Mulungu, koma Iwo watsanuliridwirapo. Koma I—Iwo sungakhoze kugwira ntchito mpaka Iwo utadzalowa mwa ife, ife anthu okhalapo, kuti ugwirire ntchito.

⁴² Ndipo mdierekezi amafuna kuti atitenge ife kuti tizigwira ntchito pansu pa iye. Chotero pamene iye akhala mwa mawonekedwe osawawa, iye amayambira mu tchimo. Ngati iye angakhoze kungowagwira iwo mongokhala munthu wolungama, munthu wabwino, ndi kungomamulola iye kuti azipitirira ndi kumayesera kukhala wabwino monga choncho; ngati iye angakhoze kumugwira iye monga choncho mpaka iye atafa, ndizo basi zomwe iye amafuna kuzichita. Iye alinaye iye, chifukwa ziribe kanthu momwe iwe uliri wolungama, momwe iwe uliri wabwino, momwe iwe uliri wamakhalidwe, momwe iwe uliri wawukhondo, momwe iwe woonamtima, iwe sudzafika konse Kumwamba mpaka iwe utabadwa kachiwiri. Yesu ananena chomwecho. Chotero palibe. . . Izo. . . Iwe uyenera kuti ubadwe, iwe uyenera kuti usinthidwe, kapena palibe njira mu dziko yoti iwe udzalowere konse Kumwamba, kapena konse—kapena kudzabwera konse kwa Khristu.

⁴³ Tsopano, ine ndinanena mphindi pang'ono zapitazo, chomwe mwina zikhoza kuwutsa mu kuganiza kwanu funso lina, kuti ine—kuti ine ndaphunzitsa, ndipo izo ndi pa—pa. . . Kuti ine sindimakhulupirira kuti ulipo wamuyaya. . . Ine aindimakhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa za gehena woyaka, mwamuyaya. Ilo silitero, chifukwa ngati gehena ali wamuyaya ndipo anthu omwe amapita uko adzalangidwa kwamuyaya, njira yokha yomwe iwo akanati adzalangidwire kwamuyaya, iwo akanayenera kuti akhale nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo umenewo uli mwa Mulungu. Mukuona? Chotero iwo adzayenera kuti adzabwere potheratu psyiti (mukuona?); ndiko, gawo lawo lachithupi lidzakhale litathetsedwa psyiti, ndiyeno gawo lawo lauzimu lidzakhale litathetsedwa psyiti. Uko ndiko kuthetsedwa kwathunthu; palibenso china kwa izo. “Osakhalaponso muzu kapena nthambi,” Baibulo limazitcha izo. Iwo athetsedweratu kwanthunthu.

⁴⁴ Ndiyeno, ine ndikhoza kutsimikizira kuti kuli miyezo Kumwamba, kuti iwo sadzakhala onse pa kufanana komweko, koma inu mudzakhala nawo Moyo Wamuyaya wofanana. Koma Baibulo limanena kuti mafumu a padziko azidzabweretsa ulemu wawo ndi ulemu (Chivumbulutso 22)—azidzabweretsa ulemu

ndi ulemerero wawo mu mzindawo. Izo zikutsimikizira kuti kudzakhala kuli mafumu mu dziko latsopano, mafumu ndi olamulira. Yesu anawauza ophunzira Ake. . . Iwo anati, “Kodi ife tidzakhala ndi chiani pamene tawasiya atate athu, ndi amayi, ndipo zonse kuti tikutsatireni Inu?”

45 Iye anati, “Indetu, Ine ndikuti kwa inu, inu mudzakhala pa mipando yachifumu khumi ndi iwiri, kumaweruza mafuko khumi ndi awiri a Israeli mu tsiku limenelo.” Mwaona, ndi china, ndi kachitidwe ka mwa dziko lapansi komwe kakubwerapo uko komwe kati—komwe kati kadzakhale kapamwamba mwapatali kwa chirichonse. Mmenemo simudzakhala muli tchimo, komabe iwo adzakhala nawo olamulira ndi ena otero mu mizinda, pamene chirichonse chiti chidzapitirizidwe mwanjira ya Moyo wa Muyaya.

46 Koma oipa adzalangidwa chifukwa cha machimo awo molingana ndi ntchito zomwe anazichita mu thupi, ndiyeno akhala kwathunthu ndi kuthetsedweratu kwapsyiti. Tsopano, musingokumbukira zimenezo. Inu omwe mukulembapo izi, kumbukirani zimenezo.

47 Ndipo ndiikeni ine pa umboni wa zimenezo, kuti pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo ife tikufunafuna umenewo; ndipo Mulungu yekha ali nawo Moyo Wamuyaya.

Palibe mitundu iwiri ya Moyo Wamuyaya, Moyo Wamuyaya umodzi, ndi wokhawo womwe umakhala moyo. Ndipo kumbukirani, ikani izi pa zozilemba zanu aponso: Chirichonse chomwe chinapangidwa, chomwe chinali ndi chiyambi, chiri ndi mapeto. Chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi chinali ndi mapeto, ndipo icho chokha chomwe chinalibe chiyambi chiribe mapeto. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chomwe sichinayambe chakhala ndi chiyambi, ndipo chimenecho chinali Mulungu. Ndipo ndiyo njira yokha yomwe inu mukanati mudzaukire mu chiukitso, ndi kukhala nawo Moyo Wamuyaya uwo mkati mwanu. Mukuona? Ndiyo njira yokha ngati inu muti mudzabwererenso, ndi chinachake chomwe chinalibe chiyambi. Ndipo pamene inu mwalandira Mzimu Woyera, mkati mwa inu mumakhala Moyo umene sunayambe konse ndipo sungakhoze konse kutha; ndipo inu mumakhala nawo Moyo umenewo mkati mwa inu, ndiye inu muli nawo Moyo Wamuyaya ndipo ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Mukuona? Ndipo inu simungakhoze konsenso kufa momwe Mulungu sangakhozenso kufa, chifukwa ndinu gawo la Mulungu.

48 Ife tinali ndi funso pano kanthawi kapitako, mkati muno penapake, la kukonzedweratu, likubweretsa izo ku chinthu chomwecho. Inu mumakhala gawo la Mulungu; ndipo ngati Mulungu anadzigawa Yekha mu Lawi Lamoto lalikulu lija, ndipo malawi aang’ono aja anapita uko pa wina aliyense wa anthu amenewo, ndipo Ilo likuchita chinthu chomwechobe

lero. Ife tikhoza kutsimikizira izo mwa chochitika chimene ife tiri nacho, mwa zophunzitsa za Baibulo, mwa kafukufuku wasayansi, chithunzi choti tizisonyeze Izo, kuti Mulungu amadzigananiza Yekha pakati pa anthu Ake. “Ndipo poti ine ndiri moyo, inu mukhala moyo nanunso,” Yesu anatero. Ife sitingakhoze kufa. Palibe chinthu chotero ngati imfa kwa Mkhristu; “Pakuti iye amene akhulupirira pa Ine, ngakhale iye akanati afe, komabe iye adzakhala moyo: Ndipo aliyense yemwe akhala moyo nakhulupirira pa Ine sadzafa konse (mukuona?)—kufa.”

⁴⁹ Mawu okuti *imfa* amatanthauza “kulekanitsidwa.” Tsopano, mwathupi, ife timalekanitsidwa ku kupenya kwathu kwathupi, chifukwa ilo likadali tchimo, koma mzimu wathu ndi wa Mulungu umene sungakhoze kulekanitsidwa kwa Mulungu, chifukwa ndife gawo la Mulungu. Ife tiri—ife tikubweretsa. . . Ife tikubweretsedwanso ku lingaliro la Mulungu lija. Chirichonse chimene Mulungu achichita ndi changwiro ndi chamuyaya. Ndipo pamene malingaliro omwe a Mulungu anatuluka kupita ku ufumu wa anthu omwe akanadzati azidzamupembedza Iye, malingaliro awo omwe ndi amuyaya. Mukuona? Iwo sangakhoze konsenso kuwonongeka. Mawu aliwonse a Mulungu ndi Amuyaya. Yesu anati, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, zonse miyamba ndi dziko lapansi zikhoza kuchokapo, koma mawu Anga sadzachoka konse.” Mukuona? Iwo ndi amuyaya limodzi ndi Mulungu. Ndipo “Ngati inu mukhala mwa Ine ndi Mawu Anga akakhala mwa inu. . .” Mukuona? Ife timakhala gawo la Mawu Ake, gawo la Moyo Wake, pakuti ndife mnofu wa mnofu Wake, ndi fupa la fupa Lake, ndi moyo wa Moyo Wake. Ndiye ife sitingakhoze konsenso kuwonongeka monga Mulungu Mwiniwake sangakhoze kuwonongeka. Ndicho chomwe Mzimu Woyera uli.

⁵⁰ Munthu wamng’ono wachoka kuno wochokera ku Georgia, M’bale Evans. Iye wakhala ali kulikonse kudutsa dzikoli. Ndipo iye ndi wothandizira wamkulu wa mzanga wabwino, Oral Roberts; ndipo i—iye anathandizira kuwulutsa kwake konse kwa pa televizioni kumeneko, ndipo zinthu zambiri iye anazichita. Koma iye anati kwa ine tsiku lina, iye anati, “M’bale Branham, ine ndinapita ku sukulu ya M’bale Jagger. Ine ndinapita kulikonse; ine ndinakakhala uko kwa miyezi itatu. Ine ndinali ndikusakasaka; ine ndinapita ku malo ndi malo, aliwonse a iwo, ndi kubwererako ndi chinthu chomwecho. Ine sindimakhoza kupeza malo pomwe ine ndinali ndi chitsimikiziro chirichonse (inu mukuona?), ngati ine ndingachite *ichi*, kapena ngati ine ndingachite *icho*, ndi chomwe ine ndingachite *apa*, kapena ine ndiri, kapena ine sindiri,” anati, “mpaka ine nditamva zophunzitsa zanu.” Anati, “Ndiye izo zinakhazikitsa izo kamodzi kwa zonse.” “Pakuti wopembedza akatsukidwa kamodzi ku machimo ake samakhalanso ndi chikumbumtima

cha tchimo.” Iye wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, ndipo iye ali nawo Moyo Wamuyaya mkati mwa iye ukukhala mmenemo ndipo sangakhozenso kufa monga Mulungu sangakhoze kufa. Ndendende Baibulo. Mukuona? Iye wasamaliridwa mwamuyaya, chifukwa iye ali nawo Moyo Wamuyaya.

⁵¹ Tsopano, izo sizikutanthauza kuti iwe ungakhoze kumachimwa ndi kudutsa nazo izo, pakuti pamene iwe uchimwa iwe umalandidwa chifukwa cha machimo ako. Kulondola ndendende. Koma utali wonse pamene Moyo Wamuyaya uli mkati mmenemo, iwe udzakhala moyo kwanthawizonse. Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga (Yohane Woyera 5:24)— iye amene amva mawu Anga, nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wosatha, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, k—koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Mukuona? Zonse. . . “Palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba; ndipo onse omwe adza kwa Ine, Ine. . . Ndipo onse omwe Atate Anga anandipatsa Ine adzadza kwa Ine.” Uko nkulondola. “Onse omwe Iye wandipatsa adzadza, ndipo palibe mmodzi wa iwo ati adzataike. Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya ndipo ndidzawautsa iwo pa tsiku lotsiriza.” (Yohane Woyera 6) O, chitsimikizo chodala chakecho. Mukuona? Ndiye inu simukusowa kuti muzipita mukuwopsyzedwa ndi imfa ndi kumadabwa.

⁵² Mulungu watipatsa ife chitsimikizo changwiwo kuti ndife ana Ake. Ndipo ngati ana Ake, Iye amatikonza ife monga momwe ine ndimawakonzero ana anga, inu mumawakonza ana anu. Pamene iwo alakwitsa, ife timawakonza iwo. N—ngati ana anga achita cholakwika, ndiye ndi udindo wanga ngati bambo kuti ndiwakonze iwo. Ndiyeno, ngati ana a Mulungu achita cholakwika, ndi udindo Wake ngati Bambo, ndipo Iye azikukonzani inu. Muzingomakumbukira zimenezo, inu muzikonzedwa. Koma utali wonse pomwe inu muli mwana Wake, dziko ndi bwino kuti lichotse manja ake pa inu (nkulondola uko!), pakuti Iye anati, “Kukanakhala bwino kwambiri kuti inu ngati mwala wa mpheru ukanati umangidwe pakhosi panu ndipo inu mukanamizidwa mnyanja yakuya kusiyana ndikuti mubweretse choipa pa mmodzi wa aang’ono awa amene akukhulupirira mwa Ine.” Uko nkulondola. Chomwe chiweruzo chimenecho chiti chidzakhale!

⁵³ Tsopano, M’bale Pat, kubwerera ku funso lanu. Mizimu yomwe inatuluka mwa munthu uja, yomwe inkamuyendetsa iye monga wamisala (mukuona?), ikuchita zinthu zomwezo lero mwa anthu. Mukuona? Ndi mizimu imeneyo, zikwi kuchulukitsa ka zikwi. Ndipo mdierekezi amabwera umu ndi chonga mpungabwi pang’ono wokha. Izo ziri monga momwe iwo amamutengera msungwana wamng’ono waku sukulu; chinthu choyamba

chimene iwo angachite ndi kumupangitsa iye kuti azisuta ndudu. Mukuona? Izo zimamuyambitsa iye. Ndipo chinthu chotsatira chimene iwo amachita, iwo amakhala amphamvu pang'ono. Ndiyeno, chinthu choyamba, izo zimathera mu chamba; ndiyeno kuchokera apo, kupitirira mpaka ku chizolowezi cha zosokoneza ubongo kwenikweni. Kodi izo zimachita chiani? Izo zimawapangitsa iwo misala. Iwo amangopenga basi, ndipo mdierekezi wawapezeketsa iwo. Mukuona?

⁵⁴ Chotero mdierekezi ali mu kusuta ndudu. Ndiwo mawonekedwe ake aang'ono osawawa. Tsopano, ngati iye awona kuti iwe ndi wanzeru kwambiri ndi kuti uchidziwa icho, iye sangalole konse kuti izo zipitilire patalinsu kuposa nduduyo. Mukuona? Bola ngati iye angakhoze kukugwirani inu apo utali wokwanira, iye awutenga moyo wanu nkuwutsekereza, chifukwa iye akudziwa kuti iwe sungakhoze kupita mpaka Mulungu atanena chomwecho. Koma iwe uzimva ulaliki pambuyo pa ulaliki, uthenga pambuyo pa uthenga, ndi nk'honya pambuyo pa nk'honya pa izo, ndi chenjezo pambuyo pa chenjezo pa izo; ndipo ngati iye angangokwanitsa kukusunga iwe motchingiridwa ndi kuika malingaliro ako pa chinachakenso, monga kukhala uli munthu wotchuka, kapena kuti iwe uyenera kukhala nacho icho, kapena chinachake chonga izo, ndiye iye amangokugwira iwe pamenepo mpaka iye atakutulutsira iwe panja. Kapena ngati iye angakhoze kungokulola iwe kuti ujowine mpingo ndi kumati, "Ine ndikakhala munthu wabwino. Ine ndikatembenusa tsamba latsopano. Ine ndikapeza... I—ine ndikupita ku mpingo uko ndi kukajowina mpingo." Ngati iye atangokhoza kukusunga iwe pansu pa izo, ndi zonse zomwe iye ayenera kuzichita. Iye wakupezerera iwe apobe, chifukwa iwe... Yesu anati, "Indetu, indetu (ndizo mwamtheradi, mwamtheradi), ine ndikuti kwa inu, kupatula ngati munthu akhala atabadwa mwa madzi ndi mwa Mzimu, iye sadzakhoza mwanjira iliyonse kulowa mu Ufumu."

Ndiloleni ine ndikusonyezeni inu chinachake. Ine ndinali kuyankhula kwa m'bale madzulo awa, M'bale Wood, pamene ife tinali paulendo, kungopita kunja, ndikusyesera kuti tipepuse malingaliro anga, kudziletsa kumayankhula kuti ndipeze mawu okwanira kuti ndidzayankhule usikuuno.

⁵⁵ Tsopano, zindikirani! Ife tikupita kumusi kuno ndi kukatenga njere yabwino yaikulu ya chimanga. Iyo ndi njere yangwiro kwambiri yomwe ilipo mu dziko lino. Tsopano, ine ndikuti...?...chimanga kapena khutu, chirichonse chomwe inu mukufuna kuchitchula icho. Ine n—ine ndichitengera icho kubwera kuno ku Clark County Fair, ndipo ine ndikawina duwa la buluu pa icho. Ndi njere yabwino kwambiri ya chimanga, chimanga changwiro kwambiri chomwe chiripo, ndinayamba ndachiwonapo. Ine ndikapeza duwa la buluu pa icho. Ine ndichitengera icho ku Floyd County; ine ndichitengera icho

ku Harrison County. Ine ndichitengera icho ku boma, ndipo ine ndichitengera icho kwa fuko. Ndipo icho chikawina duwa la buluu lirilonse. Ndi njere ya chimanga yangwiro kwambiri. Ndipo asayansi ndi magalasi awo aakulu, iwo akuyang'ana mu icho, ndipo iwo akuchipima icho. Mukuona? N... Ndi muyezo wangwiro wa potashi, ndi muyezo wangwiro wa kashiamu, n—ndi chinyezi changwiro. Chirichonse chimene chiri mu njere iyo ya chimanga chiri changwiro basi ndendende. Tsopano, inu mukuti, “Ine ndikabzala icho ndi kukadzipezera njere ina yangwiro kuchokera kwa icho.” Ndipo inu mukachibzala icho mu nthaka. Kupatula chimanga icho, njere yangwiro iyo, itakhala ndi nyongolosi yamoyo mwa iyo, iyo igona apo ndi kuvunda, ndipo awo akhala mapeto a iyo. Iyo sidzawuka aponso, ziribe kanthu momwe iyo iliri yangwiro. I—iyo sidzawuka mpaka iyo ili ndi jeremu ya moyo watsopano mwa iyo.

⁵⁶ Ndipo inu mukhoza kumutenga munthu... Tsopano, ine sindikutanthauza izi kuti ndipweteke kumverera, ine basi... Uwu ndi mpingo, uyu ndi kachisi wanga, ndipo ndine womasuka monga mbalame. Mukuona? Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzikumbukira, kuti mu izi, kuti munthu akhoza kukhala wabwino; iye akhoza kumapereka zakhumi zake; iye akhoza kukhala woonamtima; iye akhoza kumathandiza mkazi wamasiye; iye akhoza kumathandiza mwana wamasiye; iye akhoza kukhala membala wa mpingo. Inu nkusakhoza kupeza chilema chimodzi cha munthu ameneyo. Nthawi iliyonse chinachake chikati chibwerepo, amapisa mthumba lake lomwe, natenga ndalama yotsiriza yomwe iye anali nayoyi ndipo amaipereka iyo kwa osauka. I—iye adzaima ndi inu kupyola mu zowirima ndi zopyapyala. Iye adzakhala mzanu pamene ngakhale ambiri otchedwa amzanu adzakusiyani inu ndi chirichonse monga choncho; ndipo munthu ameneyo akadali kunja kwa Ufumu wa Mulungu kupatula ngati iye atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, Moyo Wamuyaya. Ndiko kulondola! Ndi momwe izo ziriri zofunikira.

⁵⁷ Ndicho chifukwa ine ndikuyesera kuti ndiwutenge mpingo wanga kuti uziwone izo. Ndipo i—ine ndikupemphera kuti inu musaganaye kuti ine ndikungoyesa kuchita ngati wanzeru pa izo. I—ine ndikuyesera kukuuzani inu kuti mdierekezi ndi wonyenga kwambiri, kuti iye ndi wonyenga kwambiri mpaka i—iye adzakupangitsani inu kumachita ngati Mkristu. Iye adzachita chinachake ndi kusanzira Khristu mpaka kwa Wosankhidwa yemwe. Baibulo linati iwo akanadzakhala oyandikana kwambiri limodzi. Inu mudzakhala munthu wabwino. Inu mudzayenera...

⁵⁸ Tsopano taonani apa, mundirole ine ndikusonyezeni inu zitsanzo kuti titsimikize tsopano. Ife tikufuna kuti tizisunge izo mwa Malemba pamene ife tiri pa mizimu iyi. Esau anali munthu wabwino kwambiri mwanjira iliyonse yomwe inu mungafune

kuzitengera izo kuposa momwe Yakobo analiri. Tsopano, Esau (Mulungu andikhululukire ine chifukwa cha ndemanga iyi), iye anali basi tambwali pang'ono. Ndizo zonse. Tsopano, ngati inu mungamuzindikire iye, anali chiani iye? Wolakatula zongomva pang'ono ndi wabodza wamkulu. Tsopano, n—ngati ine ndikunena zolakwika, Mulungu andikhululukire ine, koma iye ananama. Ndipo ananyenga, panalibe wina wonga iye nkomwe. Pamene iye anatenga timitengo tamangamanga tija ndi kutiika ito mmadzi kuti azipangitse ng'ombe za bele zija ndi nkhoa kumeneko kuti zibale nkhoa zamangamanga ndi ng'ombe zamangamanga, kuti azitenge izo zikhale zake—mmanja ake. . . Kodi iye anachita chiani? Iye anavala chikhoto cha Esau ndi chidutswa cha chikopa cha nkhoa ndi china chirichonse, ndipo anapita uko, ndipo anakamusanzira Esau pamaso pa bambo ake akhungu omwe anali mneneri. Nkulondola uko? Bwanji, iye anali shasha pang'ono; iye anali kwenikweni. Ndipo Esau anali. . . Ine si—mwina wake ine sindimayenera kuti ndinene izo mwanjira imeneyo. Mukuona? Ine sindikutanthauza izo mwanjira imeneyo. I—ine ndikubweza izo. I—iye anali—iye anali. . . ine sindikudziwa; inu mukudziwa chomwe iye anali. Mukuona? Inu mungozilingalira izo mmalingaliro anu; ine i. . . Iye anali—iye anali munthu wamkulu wa Mulungu, ndipo ine sindikufuna kuti ndinene kanthu koipa pa za iye (inu mukuona?), koma ine ndikungoyesera kuti ndilozezo zinthu za—zazing'ono zomwe iye anazichita. Tang'owonani momwe iye analiri tambwali. Wabodza? Zedi, iye anali basi—iye anali moipa. Koma kodi iye anali kuyesera kuchita chiani?

⁵⁹ Tayang'anani pa Esau. Esau anali munthu wabwino, wamakhalidwe, membala wabwino wa mpingo lero. Kodi iye ankachita chiani? Iye anali wosaka. Iye ankapita kunja. . . Ndithudi apo, umo ndi momwe iwo ankakhalira moyo. Iye ankasamalira ziweto za abambo ake. Abambo ake anali akhungu. Mneneri, mneneri wa Ambuye anali wakhungu ndipo ananyengedwa ndi mwana wake yemwe, mneneri, Isaki; kupyolera mwa iye kunadza Khristu. Inu mukhoza kumutcha iye mneneri, Baibulo linati iye anali. Ndipo anali wakhungu? Bwanji iye sanadzichize yekha? Ndipo bwanji iye sanadziwe kuti uyo anali Esau—kuti uyo anali Yakobo mmalo mwa Esau? Mukuona? Mulungu samawauza aneneri ake chirichonse. Iye amangowauza iwo chimene iye amafuna kuti iwo achidziwe. Mukuona?

⁶⁰ Mulungu anali akukonza dongosolo apo, ndipo iye ankeyenera kuti agwire ntchito mwa ilo. Mulungu. . . Ngati inu mungadzipereke nokha kwa Mulungu, Mulungu adzakupangani inu kuti muzigwira ntchito mwa dongosolo Lake lomwe.

⁶¹ Tsopano, zindikirani chimene iye anachita, chimene munthu uyu anachita. Esau anapita uko ndipo anakayesera kuti awasamalire bambo ake okalamba, osauka, akhungu; ndipo Yakobo, mwakuwoneka, iye sankasamala chomwe

chikanachitika kwa iye. Koma pali chinthu chimodzi chomwe Yakobo ankachifuna, ndipo icho chinali ufulu wakubadwa. Mosasamala chimene chikanabwera, momwe akanati awutengere iwo, muyezo womwe iye akanayenera kuti abwerepo, ufulu wakubadwa uwo unali zonse zomwe iye ankazisamala. Ndipo Esau, Baibulo limati, sanasamale za ufulu wakubadwa nawo wake; Baibulo linanena zimenezo. Ndipo Baibulo linati, “Kupatula patadza achiwerewere ena achabe pakati panu, monga munthu woipa uja Esau yemwe ananyalanyaza ufulu wakubadwa wake ndipo anawugulitsa iwo ndi chipere cha mphoza . . .”

⁶² Tsopano, kodi ufulu wakubadwa ndi chiani? Ndi ufulu. Ndi chimene ine ndikuyesera kukuuzani inu tsopano. Mzimu Woyera uwu ndi Ufulu wanu wakubadwa; iwo ndi Ufulu wakubadwa wanu. Iwo ndi ufulu wanu wopatsidwa ndi Mulungu. Tsopano, anthu amati lero, “Ine ndizipita ku mpingo. Ndine wabwino basi ngati munthu winayo. Koma ine, kumachita ngati mmodzi wa oyera odzigudubuza awo? Osati ine.” Chabwino, iwe Esau! Mukuona? Ndi chinthu chomwecho basi, kunyozetsa ufulu wakubadwa. Bwanji, iye anasinthanitsa iwo ndi chipere cha mphoza. Ndipo inu mukuugulitsa iwo . . . Tsopano, ine sindikunena kuti inu, koma dziko likuugulitsa iwo ndi zochepera kwambiri kuposa izo.

⁶³ Esau anali ndi njala. Koma, inu mukuona, ngati ubwino uti udzawerengedwe . . . Ngati winawake . . . Ngati ife tikanayenda kupita uko ndi kukakhala cha ku chihema kwa—masiku angapo, ife tikanapeza kuti Esau anali . . . Ife tikanati timusankhe Esau. Mukuona? Koma mu mtima mwake iye ankafuna ufulu wakubadwa uwo. Iye sankasamala za chinthu china chirichonse; iye ankafuna ufulu wakubadwa uwo. Ndi zonse zomwe iye ankazifuna.

⁶⁴ Ndipo Esau ankafuna kuti akhale munthu wabwino, ndi kumasamalira chirichonse, ndi kumachita chirichonse molondola basi, ndi kumapanga chirichonse basi ngati . . . Iye anali wazalamulo wabwino weniweni; Esau anali. Iye ankafuna chirichonse kuti chizikhala molondola basi. Ndipo Yakobo ankafuna chinthu chimodzi, ndipo icho chinali ufulu wakubadwa, ndipo nzonse zomwe iye ankazisamalira. Ndipo Esau . . . Inu mukuona chimene chinachitika kwa anyamata onsewo. Mukuona? Ndipo ngakhale kuchokera mwa Yakobo munachokera mbadwa khumi ndi ziwiri zomwe zinabala, chabwino, mafuko khumi ndi awiri a Israeli, kuchokera mwa Yakobo. Ndipo iye anamutcha—ndipo Mulungu anamutcha Yakobo mwana Wake yemwe. Kodi inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁶⁵ Mzimu Woyera uwo uyenera kukhala wofunikira kwambiri kwa inu kuposa china chirichonse chimene chiripo mu dziko, kutchuka kwanu, moyo wanu, ntchito yanu, chanu chirichonse

chomwe chiripo. Inu musamalekeze mpaka inu mutakhala nawo Iwo. Inu muyenera kuulandira Iwo. Iwo uyenera kukhala chopambana... Ndipo inu mukuti, “Chabwino, ine ndikuwopa i—iwo a ku ntchito yanga. Ine ndikuwopa amuna anga, anga...” Musachite mantha; lolani Iwo ukhale pa malo oyambirira. Mulole china chirichonse chipite. Mulole Iwo ukhale choyamba. “Chabwino, ine ndikuyembekeza kudzaulandira Iwo limodzi la masiku awa, M’bale Branham.” Osati limodzi la masiku awa, pano! Nthawi yake ndi ino. “Mulole Iwo ukhale woyamba ndisa—ine ndisanachite china chirichonse. Ndiloleni ine ndikhale nawo Iwo tsopano!” Kusimidwa! Izo zingathandize kuyankha funso lathu. Inu kukhala—pamene inu musimidwa pofuna Iwo, kwenikweni inu muyenera kukhala nawo Iwo kapena kufa (mukuona?), apo ndi pamene inu mungati muulandire Iwo.

⁶⁶ Myuda wamng’ono ankakhala kuno mu tawoni. Ine sindikudziwa ngati inu mumamudziwa iye kapena ayi. Iye anali atachizidwa ku khansara. Iwo anamupereka—anamuthamangitsa iye. Ndipo pamene iye anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndiye iwo anamuthamangitsadi iye, anamutulutsira iye pabwalo. Ndiyeno iye anapita nakajowina mpingo wa Methodisti. Ndipo iwo anapeza kuti iye anabatizidwa mu Dzina la Yesu, ndipo iwo anakamuika iye panja mu malo ozizira mpaka ziro, pafupi teni pansu pa ziro, mu Ohio; anamuika iye pa kama panjapo (M’bale Freeman, inu mukuyenera kumukumbukira M’bale Vance, sichoncho inu?)—anamutulutsa iye—panja uko, ndi mpope wa madzi kunja uko, ndipo anati, “Awo ndi okwanira kuti iwe ubatizidwe mu Dzina la Yesu, ine ndikulingalira.”

⁶⁷ Komabe, iye analikundiwa ine nkhani yaing’ono nthawiyina. Iye ananena kuti pamene anthu *ena* awa, mkazi wake—iwo anali kukhala nawo... Ndipo iye anali atasonkhanitsa zinthu zake zonse zakalezo mu chigalimoto chokalamba chophwanyika ndipo anayamba kupita kunja ku tawoni. Ndipo mkazi wake anati, “Kodi inu mumadziwa chiani? Ine ndimayenera kuti ndimwe madzi ine ndisanachoke ku malo awo.” Anati, “Ndiri ndi ludzu.”

Chabwino, iye anati, “Wokondedwa, apo pali mpope wa madzi.”

Anati, “Chabwino, pitirira mpaka iwe ufike pa malo abwinoko.” Inu mukuona?

Ndipo iye anapita patsogolo pang’ono, ndipo iye anati, “Pali mpope wina.”

Anati, “Chabwino, ingopitirira.” Inu mukuona?

⁶⁸ Koma anati, “Ndiye, pamene iye anafika mu dzikolo, uko kunalibe mpope.” Anati, “Iye anali kungomenyera—kufuna madzi akumwa. Ndipo anati, “Patapita kanthawi, kutali komwe

mmunda kunali mpope wakale wachimudzi, kutali komwe mmunda, kutali kudutsa gulu la ng’ombe; ndipo iye ankawopa ng’ombe.” Koma iye anati, “Iye anati, ’Levi, ine basi ndiyenera kuti ndimwe!” Chotero i—iye anaimitsa galimotoyo. Ndipo anati, iye asanafike poyiimitsa galimotoyo nkomwe, iye anali atatuluka ndipo anali akudutsa mpandawo. Iye ankayenera kuti amwe madzi. Ndipo pamene Mulungu akhala weniweni chotero kwa iwe, pamene iwe uchita ludzu chotero, kuti mwina ndi Mulungu kapena inu mufe, inu simungakhoze kupirira izo penanso, ndiye chinachake chichitika. Icho chiyenera—inu mumayamba ntchitoyo ndiye ndi Mulungu. Apo ndi pamene inu mumatenga—izo zimachitika.

⁶⁹ Tsopano, mizimu yoipa iyi imawanyenga anthu. Ndipo mizimu iyo, nthawi zambiri ili yachipembedzo kwambiri. Tsopano inu mukuti, “Inu mukutanthauza, yachipembedzo?” Inde, bwana! Ngakhale kuphunzitsa Malemba, Baibulo. Iyo ndithudi imatero.

⁷⁰ Tsopano zindikirani! Yesu anadza kwa gulu la anthu omwe anali ansembe oyera; ndipo iwo ankasunga malamulo mpaka ku lemba; ndipo iwo anali achipembedzo kwambiri, mbiri. Ndipo Yesu—Yohane anawatcha iwo, anati, “Inu m’badwo wa amamba (izo ndi njoka), ndani wakuchenjezani inu kuti muthawe ku mkwiyo womwe uli nkudza?” Pamene Yesu anawawona iwo, Iye anati, “Ndinu wa atate anu mdierekezi.” Uyo anali Mulungu akunena zimenezo. Achipembedzo basi momwe iwo akanakhalira.

⁷¹ Kumbukirani, pamene—mdierekezi amamutenga munthu wake, koma osati mzimu wake. Mulungu amamutenga munthu Wake koma osati Mzimu Woyera. Mwaona? Mzimu Woyera umabwera mu moyo wanu ndipo umawuyetsa mzimu wanu, umakhala moyo kudzera mwa inu, ndi kumakupatsani inu mphamvu kuti muzikhala moyo. Koma p—pamene mzimu wanu upitirira, mzimu wanu umasungidwa ndi Mulungu; koma Mzimu Woyera unali pa inuwo umabwera pa winawake, ndi wina wakenso, ndi winawake. . .

⁷² Mzimu uwu umene unali pa Eliya unadza pa Elisha, magawo awiri a Iwo; zaka seveni handiredi mtsogolo kapena zaka eyiti handiredi mtsogolo unadza pa Yohane Mbatizi, unamupangitsa iye kumachita. . . Taonani momwe Eliya, taonani momwe Eliya analiri: munthu wakale wokalamba waubweya, manyenje paliponse pa iye, chikopa cha nkhusa, ankawoneka ngati kambozi kaubweya, nkhope yake itatuluka monga choncho, akuyenda mwamdidi chotsika kudutsa uko ali ndi chidutsa cha chikopa atachizunguriza, lamba wake wonga—lamba kuzungulira mchiuno mwake, monga chonchi. Ngati inu mukanati. . . Ngati iye akanayendera ku nyumba yanu inu mukanati, “Uuu, mai! Itanani apolisi mwamsanga kumene. Munthu wotereyu waima patsogolo pa khomo langa.” Koma uyo

anali mneneri wa Ambuye. Zedi anali! Ndiyeno, pamene iye anafa, magawo awiri a Mzimu wake anadza pa Eliya; ndiyeno zaka eyiti handiredi kenako unadza pa Yohane Mbatizi ndipo unamupangitsa Yohane kuchita ndendende basi monga iwo ankachitira, chifukwa Iwo unali mzimu wa Eliya.

⁷³ Tsopano, ngati mzimu wa Eliya pa Yohane unamupangitsa Yohane kumachita ngati Eliya, Mzimu wa Mulungu pa inu uzikupangitsani inu kuchita monga Yesu. Tsopano, apo ndi pamene inu mukuupeza Mzimu Woyera. Mukuona? Ndi chimene Mzimu Woyera umachita. Iwo umakupangitsa iwe kufatsa, umakupangitsa iwe kudzichepetsa, umakupangitsa iwe kukhululukira.

⁷⁴ Kodi iwo akanakhoza kuzula ndevu kuchokera pa nkhope yanu, ngati inu mukanakhala muli apo, kuzikudzula izo ndi kulavulira pa nkhope yanu, pamene inu munali ndi mphamvu yoitanira—makamu a Angelo? Kodi inu mukanachita izo chifukwa cha chikondi cha kwa anthu omwe anali kulavulira pa nkhope yanu? Kodi inu mukanakhoza kuchita izo? Ngati winawake akanangoyenda kudza kwa inu kuti, “Ee, iwe wachinyengo!” ndi kukumenyani inu kumbali imodzi ya nkhope, kodi inu mukanati mupempherere chikhululukiro chawo? Tsopano, apo ndi pamene kudalira—kuyesa ngati inu muli nawo Mzimu Woyera kapena ayi. Mukuona? Pamene winawake anena chinachake choipa molakwira winawake, nthawizina yemwe amazinenera kuti ali nawo Mzimu Woyera, “Ine ndimubwezera iye ngakhale izo zinditengere ine tsiku langa lotsiriza.” Mukuona? Tsopano, apo ndi pamene iwe umafufuzira za Mzimu Woyera wako. Mukuona? “Wodala muli inu pamene anthu adzanena mitundu yonse ya zoipa molakwira inu mwabodza chifukwa cha Dzina Langa.” Koma inu mukapita kukawabwezera iwo? Ayi! “Sangalalani ndi kukhala okondwera mopitirira, chifukwa momwemo anawazunza iwo aneneri omwe analipo inu musanakhalepo.” Mukuona?

⁷⁵ Pamene winawake anena zoipa za inu, muzinena chinachake chabwino. Ngati inu simungakhoze kunena chinachake chabwino cha iwo, ndiye musati muzinena kanthu. Muzingozilola izo kupita. Mukuona? Ndiyeno, pamene inu mukhuzumuka inumwini, apempherereni iwo.

⁷⁶ Ngati pali chinthu chimodzi mu moyo wanga chomwe chandithandiza ine kuti ndizimvetsa kuti Mzimu Woyera unabwera mwa ine kumusi kuja tsiku lijali, chakhala chiri chimenecho. Ine ndinali wakupsya mtima, wowopsya, wachi Irish ku mbali zonse. Ndipo nthawizonse ine sindinkakhoza kudya nkomwe, pakamwa panga nthawizonse pankakhala posasanthidwa winawake amakhala atapapasantha ipo, kulumphira pamene ine sindimayenera kuti ndilumphire. Ine ndiri ndi mano anga ena osweka tsopano ndipo ndiwoikira pamene i—ine ndinkayankhula pamene ine sindinkayenera kuti

ndiyankhule (inu mukuona?) ndi kunena zinthu . . . Nthawizonse mu vuto. Ndipo ine ndinati. . . Winawake anati kwa ine, mphunzitsi wanga ku sukulu, iye anati. . . Ine ndinati, “Dona, i—i—ine sindingathe kudziletsa izo.” Mwaona, ine ndimalowa vuto nthawizonse. Ndipo ine ndinati, “ine sindingathe kuchitira mwina.” Mayi Temple wokalamba wosauka, iye wangopita kumene ku Ulemerero tsiku lina.

Ndipo iye anati, “Chabwino, taonani Wokonedwa.” Iye anandinyamula ine pa chilolo pake, ndipo iye anandikokera ine mmikono mwake ndipo anayamba kulira. Nthawi yoyamba yomwe ine ndinayamba ndakhalapo ndi kukonedwa monga chomwecho kuchokera kwa winawake, mkazi wachikulire. Iye anangolirira pamwamba pa ine. Iye anati, “Billy, ine ndikuchitira iwe chinachake, Wokonedwa; ine ndikupatsa iwe kachidutswa kakang’ono ka chingwe.” Ndipo anati, “Ngati aliyense wa anyamatawa alumphira pa iwe. . . .”

⁷⁷ Ankanditcha ine “wokukuta-chimanga,” chifukwa ine ndinali wochokera ku Kentucky, inu mukudziwa, n—ndipo. . . Ine ndinali—ine ndinkavala moipa kwenikweni. Ndipo iwo ankandiseka chifukwa cha tsitsi langa, likulendewera pafupi utali wa momwe ilo liriri mu tsopano, ndipo lonse pansi pa nkhope yanga. Ndipo ine ndinkangokhala ndi nthawi yoipa, inu mukudziwa. N—ndipo iwo ankakhoza kumandimenya ine apo ndi kundiwomba ine. Nthawi iliyonse aliyense akakwiya, iwo ankakhoza kuyenda nadza, ndipo basi nkundigwira ine, ndi kundiwomba ine ndigwe. Ndipo apa ine ndimabwera. Mukuona? Ndipo—chotero ndiye—ndi kumenyana. Ndipo ife tinapeza—ife tinawapatsa iwo. . . Ine mpaka ndinachita ndeu ya mpeni ndi china chirichonse.

⁷⁸ Ndipo ndinatenga mfuti ya Winchester ndi kuyesera kuiwomba iyo, kuipopera iyo pa anyamata anai kapena asanu, chifukwa chondimenya ine mpaka ine sindinkakhoza nkomwe kuima. Ndikanakhoza kumupha aliyense wa iwo ngati akanati asakhalepo Mulungu. Ndinatola zipolopolozo kuchokera pansi, ndinazibweza izo mu mfuti; izo zinkangowombera mwabwino basi monga izo zinkachitira nthawizonse. Mukuona? Ine bwezi ndiri wakupha wa anthu asanu, mwinamwake, kapena anyamata asanu.

⁷⁹ Ndinali pafupi usinkhu wa zaka khumi ndi ziwiri zokha, wokupsya mtima! Ndipo mphunzitsiyo anati, “Iwe utenge chingwe chaching’ono ichi, Billy, ndipoponse pamene upsya mtima, uzingoima ndi kumanga fundo zisanu ndi zinai mu chingwe chimenecho.” Anati, “Pamene iwe uchita izo, ndiye udzabweretse chingwe icho kwa ine. Ine ndikukulonjeza iwe kupsya mtima kwako kudzakhalakutatha.”

⁸⁰ Ine ndinati, “Akazi a Whalen, ine ndithudi ndikuganiza ndinu wabwino kwambiri.” Ine ndinati, “I—ine ndikayesera

izo.” Mukuona? (Kapena Akazi a Temple; ine ndikuti Akazi a Whalen. Ine ndinati Akazi . . . Bambo Whalen anali mphunzitsi kuno nthawi ina.) Chotero i—ine ndinaika chingwecho mthumba mwanga. Ndipo ine sindinali ndiri kuseri maminiti asanu pamene winawake anandiputanso ine. Chabwino, ine ndinapita—ndinauyamba pa iwo, inu mukudziwa. Ine ndinafikira ndipo ndinatenga chingwe changa; ndipo ine ndinayamba kuti ndimange fundo imodzi; ine ndinaponyera chingwecho pansu, ndipo uko ine ndinapita. Mukuona? Ine sindikanakhoza basi kuzichita izo. Mukuona?

⁸¹ Ndipo ine ndinati, “Ine sindingakhoze konse kukhala Mkhristu.” Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, usiku umenewo kumusi uko pa Msewu wa Ohio pamene Mzimu Woyera unadza mwa ine, izo zinathetsa kupsya mtimako. Uko kunatha. Ine ndinkati, “Ine sindingakhoze konse kuchita izo. Ine sindingakhoze kukhala Mkhristu, chifukwa ine sindimatha konse kusiyana nazo izo,” ine ndinati, “chinachake chinabadwira mwa ine.” Ine ndinati, “Mnyamata, bambo anga anali okupsya mtima; n—ndi amayi anga, theka Mmwenye, aukali wokwanira kuti nkumenyana ndi macheke.” Ine ndinati, “Ine? O, ine . . . Mnyamata, aliyense yemwe ati alumphire pa ine azilandira izo; ndizo zonse.” Ine ndinati, “Ngati ine ndingati ndikwere pamwamba pa makwerero kuti ndiwamenye iwo,” ine ndinati, “ine zedi ndingachite izo.” Mukuona?

⁸² Koma tsopano, inu mukhoza kundikhukhuluzira ine kunja uko ndi kundivwivwinyiza ine ndi . . . Mukuona? Chifukwa? Si ine! Kodi ine ndikuyesera kuti ndipange nsonga yanji apa? Chinachake chinachitika. Mphamvu yakale ija, William Branham wakale uja anafa, ndipo Winawakenso anabwera umo. Ndipo Iye amandipangitsa ine kumumvera chisoni mdani wanga. Pamene aliyense achita chirichonse cholakwika kwa ine, ine sindimapemphera konse modana nawo, ine ndimawapempherera iwo. Ndipo apo ndi pamene Mzimu Woyera unandipatsa ine kuyesa kuja usiku wina mu New England, ichi chisanachitike kumusi kuno. Pamene izo—pamene Iye anandipatsa mphamvu, anati, “Yankhula zomwe iwe ukufuna kwa anthu amenewo.” Momwe iwo anali atachitira . . . Ndipo ine ndinayang’ana pamene, ndipo ine ndinati, “Ine ndakukhululukirani inu.” Ndizo ndendende zomwe Iye ankafuna. Mukuona? Muzimukhululukira mdani wanu. Mukuona? Iyi ndi mizimu yomwe imakupanga iwe kukhala woipa. Muzisamala nayo mizimu imeneyo.

⁸³ Apa panabwera winawake pafupi. Iye anali pamwamba uko mmanda. Winawake anadzera apo, iye ankakhoza kuthamanga ndi kuwagonjetsa iwo, Baibulo linatero. Panalibe aliyense—iye anali wowopsya kwambiri mpaka palibe munthu ankadutsa ku njira imeneyo. Koma tsiku lina uko kunali Mphamvu yanyonga koposa yomwe inadutsako. Iye anali wodzazidwa ndi udani,

njiru, ziwanda, chikhamu cha izo akuyenda yenda uko, munthu wamkulu. Iwo ankakhoza kupita kumeneko, ndi kukatenga ankhondo, nkumuika iye mu unyolo; ndipo iye ankakhoza kudula maunyolo namasula. Ndi mdierekezi anali mwa iye. Apo iye anali. Iye anali . . . ? . . . Iye anali—iye akanakhala fano lenileni la kwa Jeffersonville High School. Ndithudi anali! Apo iye anali, yense wamkulu chomwechi . . . Kapena ena ausinkhu wa mmateni awa, inu mukudziwa, “O, iye ndi mwamuna weniweni.” Ine ndawawonapo anthu omwe ankalemera mapauindi thuu handiredi analibe aushi ya munthu mwa iwo. Uyo si munthu, icho ndi chirombo. Mukuona?

⁸⁴ Koma uko kunali munthu wamng’ono, wa mapewa akugwa anabwera ndi msewuwo tsiku lina, wokhala ngati wopindikira pansu (Baibulo linati panalibe kukongola koti tingamusilire Iye, usinkhu wa zaka sate ndipo atadutsa pa wa fifite), akuyenda ndi msewuwo tsiku lina. Ndipo iye anathamangira kuti akakomane naye Iye. Anati, “Ine ndingomutenga munthu wamng’ono uyu ndi kumzunguza zunguza iye.” Koma, o mai, pamene iye anakomana naye Mmodzi yu, iye anagwera pa mapazi Ake. Adierekezi awo anamudzaza kwambiri iye . . . Tsopano onani. Tsiku limenelo . . . Iye anali atagwidwa kwambiri ndi chiwanda . . .

⁸⁵ Tsopano ichi, ine ndikufuna kuti ndichiike ichi mkati umu—kwa inu. Iye anali—munthu uyo anali wodzipereka kwathunthu kwa mdierekezi, mpaka mdierekezi anagwiritsa ntchito lirime lake kuti ayankhule. Tsopano, inu mukhoza kukhala mutadzipereka kwathunthu chotero kwa Mulungu mpaka Mulungu akhoza kugwiritsa ntchito lirime lanu kuti ayankhule. Uko nkulondola! Ichu ndi chimene ine ndimadzinenera. Ulaliki uliwonse umene ine ndinayamba ndalalikirapo umene unali ndi tanthauzo lirilonse kwa iwo, ndi pamene ine ndinadzipereka, ndinamuchotsa William Branham kuti achoke panjirayo, ndipo Khristu akanakhoza kulowa mkati ndi kuyamba kuyankhula. Mukuona? Ndipo Iye akhoza kuyankhula mu chinenero.

⁸⁶ Tsopano zindikirani. Iye anali atagwidwa kwambiri ndi mzimu woipa uwo, ndipo mzimu uwo unali naye iye pafupi kwambiri mpaka . . . Ziwanda izo zinadziwa kuti nthawi yawo yafika, chifukwa izo zinakomana ndi chikondi. Mukuona? Ndipo izo zinati, “Ife timuyesa iye.” Ndipo zonse . . . Tsopano, zindikirani zomwe zinachitika. Iye anati, “Bwanji, ife tikudziwa yemwe iwe uli. Bwanji iwe uli mu thupi laling’ono longa ili, munthu wamng’ono wowoneka wowonda?” Anati, “Bwanji iwe ukubwera monga chomwecho?” Anati, “Ife tikudziwa yemwe iwe uli. Ndiwe woyerayo wa Israeli, ndipo bwanji iwe . . . ?” (Tsopano penyani! Ngati inu simukukhulupirira kuti kudzakhalapo kuzunzidwa kwa mtsogolo kwa ziwanda, mveterani kwa awa akuvomereza izo.) “Bwanji iwe wabwera kudzatizunza ife nthawiyo isanafike?” Izo zikudziwa kuti

pali kuzunzidwa kwa mtsogolo. “Bwanji iwe wabwera kuti udzatizunze ife nthawiyo isanafike.” Mukuona?

Ndipo Yesu anati, “Dzina lako ndiwe ndani?” Iye ankaliidziwa; Iye ankafuna kuti iwo alivomereze ilo.

Anati, “Ndife Legio, pakuti tilipo ochuluka a ife.” Iye anati, “Ngati iwe uti utitulutse ife kuchokera mwa munthu uyu. . .”

⁸⁷ Taonani, kamunthu kakang’ono kowonda ngati Yesu kataima pamenepo (mukuona?), ndi munthu yemwe akanakhoza kukwapula pafupi ankhondo; maunyolo sankakhoza ngakhale kumugwira iye. Mukuona, izo si nyonga zathupi. Izo si zomwe zimawerengedwa. Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera womwe uli mu moyo wako yomwe imawerengedwa. Mukuona?

⁸⁸ Iye anati, “Musati mutizunze ife nthawi isanakwane; koma ngati inu muti mutitulutse ife. . . (Penyani kuipa kwa iwo, uthakati wake.) Ngati inu muti mutitulutse ife, musati mungotilola ife kuti tizipita afulu kunjira mu dziko, chifukwa sitikudziwa ngati ife titi tikalowe mwa munthu winawakenso. Ngati inu muti mutitulutse ife. . . Iye tikufuna kuti tikakhale mwa winawake; iye tikufuna kuti tizichita chinachake; iye tikufuna kuti tizikachita kuipa kwinsano.” Uyo ndi mdierekezi. “Ine ndimbwezera iye,” [M’bale Branham akusonyezera kuipidwa—Mkonzi.] Mukuona? Uyo ndi mdierekezi. “Ine ndimubwezera iye.” Mukuona? Ingokumbukirani, ndi m’bale wanu waima apoyo, koma mdierekezi wabwera pa iye. Mukuona? “Tiloleni ife tizichita chinachake choipa. Iye tikhoza kuwapangitsa Achigadara awa kuno kuzunzika chifukwa cha ichi,” akhoza kukhala atanena kwa. . . Mkulu wa mmodzi wa iwo anati, “Tiloleni ife tipite ku gulu ilo la nkhumbe.”

⁸⁹ Yesu anati, “Yambani ulendo wanu. Koma tulukani mwa iye!” O, mai! Kamunthu kakang’ono konga ako kakuyankhula kwa khamu lalikulu ilo la ziwanda. “Tutulukani mwa iye! Inu muyenera kuchokamo.” Ndipo iwo anakalowa mwa nkhumbe izo, ndipo izo zinayamba khunyu, anazithamangitsira nkhumbe izo mu khunyu. Ndipo njira ya mmusi izo zinapita ku mtsinje, ndipo zinakamira mu mtsinje, zinakadzitsamwitsa zokha mu mtsinje. Kodi si kulondola uko?

⁹⁰ Tsopano, pamene izo zinatero. . . Ndithudi ziwandazo zinatuluka mwa izo, chifukwa izo zinazipha nkhumbe. Izo zinangozithamangitsa izo mwa khunyu. Izo zinali ndi khunyu monga wina aliyense. Kodi inu munayamba mwamuwonapo munthu ali ndi kupsya mtima? Chabwino, izo basi—ndi basi zomwe izo ziri. Ndi ziwanda zomwezo. Ndi zomwe zinachitika kwa iwo. Inu mukanati mumuwonapo mmodzi wa iwo ali ndi kupsya mtima, inu mukanati, “A ha, ine ndikudziwa zomwe zinachitika ku Gadara tsopano.” Mukuona? Ndizo basi ndendende. Zochepa zokha kuonjezerapo zitabwera apo, zingamupangitse iye misala kwathunthu; chifukwa adokotala

azamankhwala angakuuzeni inu kuti kupsya mtima ndi gawo loyamba la misala. Ndi chimene Mayo amanena, gawo loyamba la misala.

⁹¹ M'bale Pat, izo zikhoza kukhala mwa mwano. Ndizo mwakukhoza momwe ine ndikuzidziwira, basi mosayembekezera. Chabwino.

102. Aroma mutu wa 7, ndime ya 25.

⁹² Ine ndiyenera kuti . . . Ine ndaiwala, ine ndinaziyang'ana izo tsiku lina pamene ine ndinalilandira ilo, koma ine ndaiwala basi chomwe izo ziri. Tiyeni tiyankhe funso la munthu wokondeka uyu ngati ife tingakhoze. Aroma 7:22, chabwino. Twente faifi, ine ndikupempha chikhululukiro chanu. Aroma 7 . . . Ine ndinatembenuza masamba awiri mwa kamodzi apo. Mukuona?

Ine ndikuthokoza Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Kotero kuti—kotero ndiye ndi malingaliro—ndi—malingaliro ine mwiniwanga ndimatumikira lamulo la Mulungu; koma ndi mnofu lamulo la tchimo.

Tsopano, dikirani miniti. Ine sindinawerenge izo molondola kumene.

Ine ndikuthokoza Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Chotero ndiye ndi malingaliro . . . (Eya, ndiko kulondola.) . . . Ine mwiniwanga ndikutumikira lamulo la Mulungu; koma ndi mnofu lamulo la tchimo.

⁹³ Chabwino. Ndi ndendende zomwe Paulo ankanena nthawizambiri mobwereza. Pamene ine ndikanati ndichite chabwino, choipa chiri pamenepo. Mukuona? Ndizo ndendende zomwe inu mumachita nanunso. *Ndi malingaliro anu*, uwo ndi mtima wanu. Mukuona? Tsopano kumbukirani, inu simumaganiza ndi malingaliro anu; ngakhalenso simumapenya ndi maso anu. Ngakhalenso sikuti inu—m—mu . . . Inu mumawona ndi mtima wanu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Kodi munadziwa kuti mtima wanu uli ndi munthu wina mkati mwake pambali pa inumwini? Sayansi yangopeza kumene izo pafupi zaka foro zapitazo, inu mukudziwa. Kachipinda kakang'ono mu mtima, iwo amati solo imakhalamo.

⁹⁴ Kodi inu munayamba mwamvapo za chikumbumtima? Inu mukayamba kuchita chirichonse, ndipo inu nkumaganiza, “O, ine ndikungokwera pamwamba pa izo,” koma chikumbumtima chanu chimakuuzani inu mosiyana.

⁹⁵ Iwo akhoza kutenga chodziwira bodza . . . Ine ndikumuwona mzanga wabwino, Woimira mlandu Robinson, wakhala mmbuyo umo. Ndipo ine sindikudziwa ngati inu munayamba mwaziwonapo izo zikuchitidwa kapena ayi, koma ine zinachitika kuti ine ndinali nacho icho—kuyesa—icho

chinaikidwapo pa ine nthawi ina, zokhudza Mngelo wa Ambuye uyu kuno. Ndipo iwo amaika chodziwira bodza pa iwe, ndipo iwe umayesera—kuti uvomereze mwakupambana kwa kudziwa kwako, mopambana momwe iwe ungakhoze kuchipangira icho, mwabwino kwambiri basi ndi mokometserapo, kuti iwe sunachite chinthu *chakuti-n-chakuti*—mulandu. Chodziwira bodza icho chimapotokera mmbuyo momwe ndi kuti iwe ukunama. Mukuona? Bwanji? Ndi kunjenjemera kwa misempha yako komwe iwo amakupeza pa chodziwira bodzacho. Mukuona? I—icho chingakuuzeni inu. Chifukwa chiani? Munthu sanapangidwe kuti azinama mu uchiyambi wake wapachiyambi. Ndi tchimo ndi mdierekezi yemwe ali pa inu yemwe amakupangitsani kuti muname. Mukuona?

⁹⁶ Inu simuna—mapangidwe anu si oti muzinama. Ndi chifukwa inu muyenera kuti mudzakhale moyo kachiwiri, chifukwa inu munapangidwa, munalengedwa kuti muzikhala moyo kwanthawizonse, kukhala moyo nthawizonse. Koma onani, tchimo linabwera umu ndipo linabweretsa imfa kwa thupi. Ndiyeno, pamene tchimo libwera umu ndi kubweretsa imfa kwa thupi, ndiye ndithudi, thupi liyenera kuti life. Koma ilo—mkati umu mukhoza kumakhala Moyo Wamuyaya, pamene mzimu uwu usinthidwa mkati mwanu ndipo inu mumakhala ndi Moyo Wamuyaya. Mulungu adzaliutsa thupi limenelo kachiwiri pa tsiku lotsiriza. Iye anati Iye akanadzachita izo.

⁹⁷ Chotero ndi malingaliro anga—malingaliro...Iye anati mu malo ena, “Ine ndikuganiza ine ndiri nawo malingaliro a Khristu.” Tsopano, mu malingaliro amenewo inu mumatumikira—ndi malingaliro a Khristu inu mumatumikira Mulungu. Mukuona, gawo la mkatilo (mukuona?), gawo la mkati, inu mumatumikira Mulungu. Chikumbumtima icho, umu ndi momwe chikhulupiriro chimakhala.

⁹⁸ Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu. Kodi pali nthawi yochuluka yomwe anthu inu kuno, ambiri a inu mwawonapo nthawi pamene inu m—inu mumangodziwa chinachake chikuti chichitike. Izo zimawoneka ngati izo zikanakhala zosatheka, koma inu munatero, mumangodziwa kuti izo zikanati zichitike. Kodi inu munayamba mwakhala nazo? Icho ndi chikhulupiriro chimenecho, chikumbumtima icho chikugwira ntchito.

Tsopano, ngati mukuyamba kutentha pang’ono muno, inu mukhoza kutembuzira chosinthira icho panso apo, ngati muno mukutentha kwambiri pang’ono kwa inu.

⁹⁹ Tsopano, mkati umu chikumbumtima icho (mukuona?), apo ndi pamene malingaliro anu. . . Tsopano Yesu anati, “Kupatula munthu akhale atabadwa kachiwiri. . .” (Tsopano, si zomwe ine ndimafuna.) “Indetu, indetu, ine ndinena kwa inu, kupatula munthu akhale atabadwa kachiwiri iye sangakhoze *kuwuona* Ufumu wa Mulungu.” Tsopano, inu simukanakhoza kuwuona

Ufumu wa Mulungu, chifukwa Ufumu wa Mulungu ndi Mzimu Woyera. “Ena aima pano sadzalawa imfa mpaka iwo atawona Ufumu ukubwera mu mphamvu,” Iye anatero. Ndiye, “Ufumu wa Mulungu,” Baibulo linati, “uli mkati mwanu.” Uli mkati mwa inu, Mzimu Woyera, ndipo inu simungakhoze kuwuona iwo ndi maso anu. Chotero *kuwona* kumatanthauza “kumvetsa.”

¹⁰⁰ Kodi inu munayamba mwayang’ana pa chirichonse, nkumayang’ana kumene pa icho, nkuti, “Chabwino, ine basi sindikuchiwona basi icho.” Mukuona? “Ine sindikuchiwona basi icho.” Inu mukutanthauza simukuchimvetsa icho. Mwaona, mukuona? Inu simukuchimvetsa icho. *Kuwona* ndi “kumvetsa.” Koma ndi maso anu inu mumayang’ana pa chirichonse. Koma ndi chimene chiri mkati mwa inu, inu mumamvetsa icho, inu mukuona ndi umo. Mukuona? Ndi maso a Mulungu inu mumayang’ana.

¹⁰¹ Ndipo tsopano, gwirani nsonga yanu tsopano. Apa pali china chabwino ngati inu mwakonzekera icho: Mkhristu amayang’ana pa zinthu zomwe iye samaziwona ndi maso ake (mwaona?), pakuti ife timayang’ana pa zosawoneka. Mukuona? Kodi inu mumayang’ana chotani pa izo? Ndi maso anu amkati. Inu mumaziwona izo mwa chikhulupiriro. Ndipo tsopano, kuti titsimikizire izo: zida zonse za Chikhristu zapangidwa ndi zikhalidwe zosawoneka. Kodi zida Zachikhristu ndi chiani? Winawake akuti, “Kuwona ndi kukhulupirira.” Munthu ameneyo sangakhoze konse kukhala Mkhristu, chifukwa zida za Chikhristu zapangidwa ndi izi: chikondi. Kodi inu munayamba mwachiwonapo icho? Inu munachionapo icho chikuchitika, koma inu simunayambe mwachiwonapo chikondi. Inu simungakhoze. Kokani gawo lanu la chikondi ndi kulola ine kuti ndiwone kuti chimawoneka motani. Mukuona? Chikondi, chikondi, chisangalalo, mtendere, kupirira motalika, ubwino, kufatsa, chikhulupiriro—chikhulupiriro, chifatso (mukuona?); zida zonse za Chikhristu ndi zosawoneka ndi maso achibadwa, koma izo zimamvetsedwa ndi mtima! Ndi inu apo. Ndi inu apo.

¹⁰² Paulo anati ndiye, “Ndi malingaliro anga... (Ndipo ine ndiri nawo malingaliro a Khristu...?...) iye anati.) Ine ndimamutumikira Mulungu ndi malingaliro anga, koma thupi langa (kodi iye anayankhula chotani izo pamapeto?)—koma ndi mnofu, lamulo la tchimo.” Kodi ndi chiani icho? Thupi langa likuti usikuuno, “Iwe watopa kwambiri. Mmero wako watupa kwambiri. Iwe uli—Iwe wakhala uli kunja uko mu mphepo lero. Iwe usapite ku tchalitchi usikuuno.” Ilo ndi lamulo la thupi. “Iwe mwina ukhoza kungowaimbira iwo ndi kumuuza M’bale Neville kuti... Kutumiza mafunsowo uko ndi kumuuza iye kuti awayankhe iwo.” Koma inu mukuona, ine ndinalonjeza kuti ndichita izo. Mukuona?

¹⁰³ Tsopano, malingaliro anga, mkatimu Mzimu Woyera unati, “Iwe usunge lonjezo lako.”

Koma thupi limati, “Iwetu watopa kwambiri.” Mukuona?

¹⁰⁴ Tsopano, thupi limati, “Tsopano, palibe kufunikira, iwe kanthu kakang’ono kokongola, ndiwe kanthu kokongoletsetsa kakang’ono mu sukulu. Tsopano, usati uziperka tcheru chirichonse kwa mayi wako woyera wodzigudubuza uyo kapena bambo wako wotentheka uyo. Mukuona? Iwe ndi msungwana wowoneka bwino kwambiri mu sukulu.” “Ndiwe mnyamata wokongola kwambiri, mnyamata wowoneka bwino kwambiri, wowumbidwa bwino kwambiri. Ndiwe wotchuka kwambiri yemwe alipo mu mzindawu.” Inu mukuona? I—izo. . . Ndipo iwe umapereka ziwallo zako kwa izo, ndipo kodi iwe umathera pati? Pa mapeto aang’ono a nyanga nthawi iliyonse. Mukuona?

¹⁰⁵ Paulo anati, “Thupi langa limafuna kutero—limafuna nthawizonse kuti lidziperekere kwa izo.” Thupi lanu limatero nalonso. Mukuona? Koma lamulo la Mzimu wa Mulungu mu mtima limagonjetsa thupi ndi kulipangitsa thupi kuti limvere chomwe mtima ukunena kuti lichite. Aleluya!

¹⁰⁶ Penyani, ndiye ngati izo zingachite izo kwa wochimwa, ndiye kodi izo sizingagwire ntchito kwa matenda aponso? Lamulo la Mzimu wa Mulungu mu mtima umene umadziwa kuti “Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa,” iwo amaima ndi mphamvu yawo kuti apangitse matenda awo mu thupi ilo kuwamvera iwo, chifukwa ndi mdierekezi. Ndi inu apo. Pfyuu! Izo ziri ndi zonona pa izo mwakuya choncho. Ine ndikukuuzani inu. Ndi zimenezo. Mwaona?

¹⁰⁷ Tsopano, lamulo la tchimo ndi imfa limagwira ntchito mu mnofu wanu, koma lamulo la Mzimu wa Moyo limagwira ntchito mu mtima mwanu. Kotero mtima wanu, mzimu wanu mu mtima wanu umapangitsa thupi lanu kumvera chomwe ilo likutichita. Ndizo ndendende kulondola. Tsopano, izo ndi zomwe Paulo ananena. Nthawizonse mnofuwu, “Ine ndatopa kwambiri; ine sindikwanitsa; ine sindiri wokwanira; ine sindingakhoze kuzichita izo.”

Ine ndinati kwa—kwa Loyce kuno, kapena Dolores, kapena winawake yemwe wakhala akuyankhula kwa ine zokhudza Mzimu Woyera, zokhudza chinachake kapena china monga choncho, ine ndinati—ndinati, “Nchiani. . .”

Dolores anati, “Chiani—nchiani chinandipangitsa ine kuti ndimverere mwanjira imeneyo basi pa nthawi yomwe ine ndikanati ndimverere mwabwino?”

¹⁰⁸ Ine ndinati, “Mdierekezi. Iye anakuwona iwe kuti unali wokonzeka kuti uwulandire iwo. Iye anati, ‘Ine ndiyika choziziritsa pang’ono pa iye [M’bale Branham akupanga phokoso kuti afotokoze—Mkonzi.], kumupemerera iye pang’ono pokha, inu mukudziwa, kukhala ngati kuziziritsa pang’ono.’ Mukuona? Koma o, mai, apo ndi pamene iwe umauka! Kutenga maufulu ako opatsidwa ndi Mulungu.” Ndi zomwe Paulo anali

kutanthauza. Mukuona? A... “Nthawizonse pamene—” iye anati, “pamene ine ndifuna kuchita chabwino, choipa chiri pomwepo.”

¹⁰⁹ Ndikuuzeni inu choti muzichita. Ine ndazindikira ichi, mkazi wanga ndi ine. . . Ndipo ine ndingofulumira nkubwerera, chifukwa ine ndangokhala ndi maminiti pang’ono motalikirapo, ndipo ine ndiri ndi mafunso aakulu pano. Ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu mochedwa kwambiri, koma ine ndikufuna kuti nditenge mafunso anu mwakukhoza kwambiri momwe ine ndingathere.

¹¹⁰ Zindikirani! Ine ndikhoza kuyambira mmawa, nkuti ine ndikupita. . . Tsopano, Ambuye akunditsogolera ine kuti ndipite ku malo ena ake ku msonkhano, chabwino, m’bale, inu mungopenya chirichonse chikuchitika. Kapena munirole ine ndipite kwathu, ndipo kuitana kwa kutali kwinakwake kubwere umu. Tsopano, ine ndiyenera kuti ndipempherere odwala. Joseph wamng’ono akwera pamwamba pa khosi langa. Sarah akufuna kuti andifunse ine funso. Becky ayamba palimba. Ine ndikati, “Shi, shi, shi!” Kuikapo dzanja langa, “Hei, shi, shi, shi, ine ndikuti—Adadi akuti apempherere odwala.”

“Chabwino, Adadi, taonani; Joe wachita izi. . .” Inu mukuona? Kungoti izo ziyambike. Ndipo mwamsanga pamene pempherolo litha, iwo amatenga zidole zawo ndi basi mokoma ndi mwabwinobwino. Ndi mdierekezi. Ndithudi ndi iye.

¹¹¹ Ndiyeno ine ndimabwera apo nkudzati, “Joseph, iwe usamachite chinthu *chakuti*.” Ndipo inu mukudziwa, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye walowa mu chizolowezi. Ndipo inu mumazipeza mwa ana anu, iwo amanama kwa inu. Chabwino, uwo ndi mzimu wonama pa mwana ameneyo. Pali mankhwala amodzi okha kwa izo. Ndodo ya mfuti sindiyo lingaliro langa, inu mukudziwa, shamboko yomwe ife tinkakwapulidwa nayo, M’bale Jess. Pamene ife tinka—tinka—tinkakhala mu vuto ife tinkakonda kukwapulidwa ndi shamboko yochokera mu mfuti zakale, ndodo ya hikore, inu mukudziwa, zida zakale zothira onga. Ilo si lingalirolo. Koma pemphero, limathamangitsira mdierekezi woipa uyo kutali ndi mwana uyo. Ndiko kulondola. Pemphero limachita izo.

¹¹² Ngati Molly wamng’ono angoyamba kupondetsa phazi lake laling’onolo, ndi kumathamangira panja, ndi kumalozetsa mmwamba mphuno yake yaing’onoyo, inu mukhoza kumamumenya iye mpaka iye osakhalanso ndi malaya aliwonse pa iye; iye azachitabe izo mulimonse. Koma inu mungoziyika pamaso pa Mulungu ndi kuitanira moyo wa mwana ameneyo kwa Mulungu. Mkungokhala apo pomwe ndi icho. Ine ndikukhulupirira ndi chinthu chopambana chimene ine ndikuchidziwa. Inde, bwana! Ndiwo mankhwala opambana omwe ine ndikuwadziwa, ndilo pemphero.

103. Tsopano, tiyeni tiwone. Tsopano lotsatira lina pano likuti, **Kodi chikutanthauzidwa nchiani pakuti kukonzedweratu dziko lisanayambe; kodi ziri pati mu Baibulo?** Kukonzedweratu dziko lisanayambe nkomwe?

¹¹³ Chabwino, bwenzi langa lofunika, tiyeni ife titembenuzire ku Aefeso mutu woyamba mwa malo amodzi okha. Ife sititenga motalika kwambiri pa ili ine sindikuganiza, kupatula ngati sipakuyankha molondola. Ndipo tiyeni tingoyamba kuwerenga apa pa Aefeso mutu woyamba.

¹¹⁴ Tsopano, chinthu choyamba, ine ndikufuna kuti ndinene ichi, kuti *kukonzedweratu* ndi mawu oipa kwa mtumiki k—kuti awagwiritse ntchito pamaso pa gulu losaphunzitsidwa. Mukuona? Iwo ali. Ine sindimawagwiritsa iwo ntchito. Nthawizina kuno ku tchalitchi. . . Koma kunja mwa omvetsera, uko mwamukulu. . . Komwe c—chirichonse chimawunjikidwa kuchokera mu chirichonse, ine ndimawapenyeseza mawu amenewo. Ine nthawizonse ndimagwiritsa ntchito mawu oti *kudziwidwiratu*, chifukwa kukonzedweratu ndi kudziwidwiratu kwa Mulungu kokha. Mulungu pokhala wopandamalire, mwa kudziwiratu Iye anadziwa chirichonse, kapena Iye si wopandamalire. Mukuona, mukuona? Iye ankadziwa chomwe chikanati chidzachitike. Chotero mwa kudziwiratu Iye akanakhoza kukonzeratu. Ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira kuti Mulungu—kuti Mulungu samangoti. . .

¹¹⁵ Monga ngati mpweya womwe inu mukupuma; ine sindigwirizana nawo a Mboni za Yehova pa lingaliro limenelo kuti mpweya wanu ndi mzimu wanu. Izo sizingakhoze kukhala. Mukuona? Mzimu wanu uli mu mtima mwanu. Mukuona? Ndipo inu munali ndi mzimu wanu musana—bwere konse mu dziko. Mulungu anamuuzza Yeremiya kuti Iye anamudziwa iye, ndipo anamuyeretsa iye, ndipo anamupanga iye mneneri wa pa fuko—wa pa mafuko asanayembekezedwe konse mu chiberekero cha amayi ake (mukuona?), Yeremiya 1:4.

¹¹⁶ Tsopano zindikirani. Chotero ife tikuwona kuti zinthu zonse izi ziri mkudziwidwiratu. Zaka seveni handiredi thwelofu Yesu asanabadwe—Yohane asanabadwe, Yesaya anamuwona iye mu masomphenya, anati iye anali liwu la mmodzi wofuula mu chipululu—zaka 712. Kuyambira mmunda wa Edeni, Yesu Khristu, asanaikidwe maziko a dziko. . .

¹¹⁷ Anachita bwanji. . .? Tiyeni tiwerenge izi. Aefeso 1, tiyeni tingoyambira pa mutu wa 1 chotero—kapena ndime yoyamba.

Paulo, mtumwi. . . (Tsopano penyani momwe iye akuwayankhulira awa. Ine ndimaikonda njira iyi ya Paulo. Ine ndimamukonda Paulo, simutero inu? O, iye anali wantchito wodabwitsa wa Khristu. Tsopano penyani izi.)

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, kwa oyera omwe ali ku Efeso, ndi... okhulupirika mwa Khristu Yesu.

118 Zindikirani, izi sizikulembedwera kwa dziko; izi sizikulembedwera kwa akunja. Izi ndi za kwa Mpingo womwe uli mwa Yesu Khristu (o, kodi izo si zokondeka?), Mpingo mwa Yesu Khristu. Ndizo...Kodi mumalowa chotani mwa Yesu Khristu tsopano? Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi. Tsopano—momwe...N—ndipo iye akulondolera izi kwa anthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera (mukuona?), osati kwa dziko lakunja.

Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, kuchokera kwa Mulungu Atate athu, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu.

Wodala akhale Mulungu Atate wathu—Mulungu ndi—Atate wathu wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife mu malo onse ammwambamwamba—ndi madalitso auzimu mu malo ammwambamwamba mwa Khristu!

119 O, mai! Kodi inu simungakonde kukakhala mwa ena a iwo? Chabwino, ife tiri. Zedi! Mzimu Woyera womwewo. Anati tsopano, pamene inu mukukhala limodzi mu malo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, Mulungu watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu, Mlono Rose. Ine ndikukhulupirira—kuti—izo...I—ine sindikanakhoza kuliganizira dzina lanu tsiku lina. Ine ndikukhulupirira inu munali mu mzere wa pemphero kapena chinachake. Ndipo i—ine ndikukumbukira ndikuyesera kuti ndiganize za ilo kenako, ndipo ine—koma dzina lanu ndi Rose Austin, si kulondola uko?...?... Inu kunkabwera kuno ku kachisi nthawi zonse. Ndi zimenezo. Chabwino. Tsopano:

Wodalitsidwa akhale—Mulungu wa Atate wathu wa...Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu—mzimu wonse—mu malo ammwambamwamba... (Tiyeni tiwone ngati ine ndikuwerenga izo—kubwereza izo molondola.)

Adalitsidwe Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mu malo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu: (Tasonkhana limodzi tsopano mu malo ammwambamwamba mwa Khristu Yesu.)

Malingana ndi momwe iye... (Tsopano mveterani! Kodi inu nonse mwakonzeka?)...Malingana ndi momwe iye anatisankha ife mwa iye kale... (Ine ndinalalikirira kwa inu)...asanaikidwe maziko a dziko,...

¹²⁰ Tsopano, onani, iye akhoza kuyankhula kwa Mpingowu. Iye sakanakhoza kunena izo kwa makanda, koma iye akuyankhula kwa Mpingo womwe uli kale mwa Khristu. Tsopano, iye sangakhoze kupita kunja kuno basi kwa mpingo winawake nkuti, “Chabwino tsopano . . .”—izo. Ndi osankhidwa Awo omwe ali mwa Khristu.

¹²¹ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti ine ndiri mwa Khristu.” Ngati inu muli, inu mwalandira Mzimu Woyera, chifukwa ndi njira yokha yomwe inu mungakhoze kulowera mwa Khristu. I Akorinto 12:13 (mukuona?)—I Akorinto mutu wa 12. Chabwino. “Pakuti ndi Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi (lomwe liri Thupi la Khristu.” Tsopano! Ndiye ife timakhala limodzi mu malo ammwambamwamba mwa mtima umodzi, Mzimu Woyera ukuyenda pakati pathu, ukutiphunzitsa ife, kutisonyeza ife zinthu zazikulu, kubweretsa zinthu pa kuchitika. O, malo akewo.

¹²² Iye anati, “Tsopano, inu amene mwaitanidwa monga chomwecho, ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa inu, inu omwe muli osankhidwanu. Pomwe Mulungu anatisankha ife mwa Iye asanaikidwe maziko a dziko, taganizani za zimenezo. Mulungu anatisankha ife mwa Iye asanaikidwe maziko a dziko. Mulungu anadziwa asanaikidwe maziko a dziko kuti ine ndikanadzayankhula phunziro lomweli usikuuno. Iye ndi wopandamalire. Ndipo kusanakhale konse dziko . . . O! Psfyuu! Landi—landirani Mzimu Woyera tsopano. Mawu awubweretsa Iwo. Mukuona? Umo ndi momwe Iwo unabwerera: “Pamene Petro ali akuyankhula mawu awa Mzimu Woyera unagwera pa iwo.”

¹²³ Kusanakhale dziko inu munali mu malingaliro a Mulungu kuti adzakupatseni inu Mzimu Woyera, chifukwa Iye anakdziwa kuti inu mukanadzamausowa Iwo; ndipo Iye anakusankhani inu Iyemwini chifukwa inu munkaukhumba . . . Iye anakusankhani inu mwa Khristu inu musanati kapena Yesu, aliyense wa inu, asanakhale pa dziko lapansi. Ndipo Iye anatuma Yesu kuti adzafe, kuti adzakonze njira yotumizira Mzimu Woyera, kuti adzakubweretseni inu kwa Iyemwini. O, ndizo basi . . . Ine ndikudziwa ine ndikhoza . . . Uno ndi mpingo, chotero ine ndiri kwathu tsopano. O, izo ndi zolemera kwambiri kwa ine. Kuganiza kuti si zomwe ine ndinkafuna; izo sizinali zokhumba zanga; izo sizinali zofuna zanga; iko sikunali kusankha kwanga; ine ndinalibe chinthu chimodzi chochita nazo izo. Koma dziko lisanayambe konse, Mulungu anatiwona ife ndipo anaika dzina lathu pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Kusanakhale konse dziko! Mukanena za Mulungu! Psfyuu!

¹²⁴ Ine ndinaima kunja kutali komwe kwa galasi lalikulu ilo . . . Inu mukhoza kuwona zaka handiredi ndi twente milioni za danga la kuwala. Pamene ine ndinayang’ana ndi kuziwona

izo (ine sindinafike powona kupyolera mu galasi, koma ine ndinawona chithunzi pamene iwo anachitenga icho)—ndipo ine ndinayenera basi kuti ndikweze manja anga mmwamba apo, mu malo amenewo, ndipo ine ndinati, “Ndinu wamkulu bwanji, Ndinu wamkulu bwanji!” Ndipo limodzi la maiko awo lisanatembenuke nkomwe (Aleluya!), Mulungu anatisankha ife mwa Yesu Khristu. Tsopano, Ndinu wamkulu bwanji. Inde, bwana!

¹²⁵ Kusanakhale konse dziko, kusanakhale konse mpirawu, kusanakhale konse dzuwa, kusanakhale konse mwezi, kusanakhale konse kuwala, kusanakhale konse chirichonse, pamene kunali kuli Mulungu yekha, Mulungu ndi malingaliro Ake, malingaliro amuyaya a Mulungu anakusankhani inu mwa kukonzeratu, mwa kudziwiratu, ankadziwa kuti inu mukanadzakhala pa dziko lapansi, ankadziwa kuti pakanadzakhala tchimo.

¹²⁶ Winawake akuti, “Ndiye, bwanji anatero—bwanji uko kunakhala tchimo?” Ngati kukanati kusakhale tchimo, mzokhumba Zake sibwezi patadzakhala Mpulumutsi. Pankayenera kukhala pali wochimwa chotero kuti Iye akanakhala Mpulumutsi. Pankayenera kuti padzakhale munthu wodwala chotero kuti Iye akanakhala Mchiritsi. Amenii! Ndi inu apo. Izo zinkayenera kuti zidzakhale mwanjira imeneyo. Uyo anali Mulungu y—yemwe anaziwona izo ndipo anazidzozeratu izo. Mdierekezi sali konse mu mpikisanowo. O, iye ali chabe chinthu cha pambali pa msewu chomwe Mulungu anachigwiritsa ntchito kuti awabweretsera ana kwa Iye, akufuula, “Abba, Atate.” Palibe zodabwitsa pa tsiku limenelo momwe Angelo ati azidzaimbira! Pamene ife tidzaimba nkhanu za chiwombolo, Angelo adzaweramitsa mitu yawo; asakudziwa zomwe ife tikuzikamba. Zedi! Iwo sanayambe atayika konse. Iwo sadziwa chomwe chiri. Iwo sakudziwa momwe ife tikumverera bwino, podziwa kuti ife omwe nthawiyina tinakhalapo ochimwa ndipo tinatalikirana ndi Mulungu, opanda chiyembekezo, opanda chifundo, opanda Mulungu mu dziko la chivundi, tikufa, tikupita ku gehena ya mdierekezi; ndipo Mulungu anaweramira pansu, ndipo anatinyamula ife, ndipo anatiwombola ife; ndipo tsopano ife tiri pamwamba pa Angelo. Pakali pano!

¹²⁷ Nchiani icho? Mngelo ndi wantchito. Ndife ana aamuna ndi aakazi. Kodi yemwe amaganiziridwa kwambiri ndi ndani, wantchito wako kapena mwana wako wamwamuna kapena wamkazi? O, mai! Pemphero lochokera kwa woyera lidzapita nthawi kamilioni patali kuposa Mngelo (inde, bwana!), chifukwa iye ndi mwana. O, uko nkulondola, m’bale wanga, mlongo.

¹²⁸ Inu musamati...Mpingo...Ine sindimakhulupirira mbali iyi ya umuyaya momwe ife titi tidzazindikirire konse chomwe iwe uli, udindo womwe iwe uli, umene Mulungu wakuikapo

iwe, anthu odzazidwa-Mzimu inu. Inu ndi ana aamuna a Mulungu. Pakuti, Mngelo ndi wantchito. Ndinu mwana wamwamuna! Mngelo akhoza kungokubweretserani inu uthenga, koma inu muyenera kumachitapo. Amen! Ndinu wochitapo powonekerapa. Ndinu mwana wamwamuna. Angelo ndi antchito kuti azikubweretserani inu uthenga. Kuti apa, “Ine ndakubweretserani inu uthenga uwu kuti inu muchite *zakuti-n-zakuti*. Izi ndi zochokera kwa Atate. Ine ndaubweretsa iwo kwa inu. Inde!” Ndi zonse zomwe ziri. Amen! Ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Anatikonzeratu ife! Tsopano, penyani miniti yokha.

Monga momwe iye—iye anatisankha ife... (Tsopano, ife sitinasankhe... Ine ndikanakhoza bwanji kumusankha Iye? Zaka mabilioni mazana anai, milioni, bilioni, zaka trilioni zapitazo, ine ndikanakhoza bwanji kumusankha Iye? Koma Iye anandisankha ine. Amen! O, M'bale Wood, ndi zimenezo. Mukuona?)... anatisankha ife mwa iye asanaikidwe maziko adziko, kuti ife tikhale tiri oyera... (Tsopano, musati muyesere kuzipanga izo mwanokha, chifukwa inu simungathe)... ndi opanda chilema pamaso pa iye mu chikondi:

O, m'bale, izo ziyankha funso lomwe ine ndinaliona muno maminiti pang'ono apitawo. Penapake i—ine ndinaliona ilo basi... O, inde. Inu munati:

Kodi munthu angakhoze bwanji kumakhala moyo wa pamwamba... kukhala pafupi kwambiri ndi Mulungu, iye nkukhala wopanda tchimo? Mvetserani kwa izi.

...woyera... kuyambira ku maziko a dziko, kuti ife tikhale oyera ndi opanda chilema pamaso pa iye mu chikondi:

¹²⁹ Chikondi chake chinachita izo. Chikondi chake chinalipirira machimo anga. Chikondi chake chinachotsera iwo kutali. Chikondi ndi kukankha kwamphamvu kwambiri komwe kulali. Mukamutenga mwamuna yemwe amamukonda kwenikweni mkazi wake, iye angamufere iye mwaufulu. Ndipo chikondi chapaabale...

¹³⁰ Kunali munthu, munthu winawake, amabwera ku mpingo uno kamodzi mu nthawi, wakutali uko mu dziko. Anali atakhala pa nyumba ya m'bale wake tsiku lina. Iye anati “Bwanji ngati chinachake chitachitika kwa M'bale Bill?” Iye anati, “Mokondwera ine ndikanatulutsa chidali changa kuti andiwombere ine mmalo mwake.” Mukuona? Kukufera iwe. Icho ndi chikondi. Chikondi choposa munthu alibe choposa iwo omwe angaika moyo wawo pansu chifukwa cha—m'bale wake. Mukuona?

131 Mu chikondi, anatisankha ife mu chikondi asanaikidwe maziko a dziko. Tsopano penyani:

Atatikonzeratu ife... (Tsopano, apo pali mawu oti kukonzedweratu.)... Atatikonzeratu ife kuti tidzakhazikitsidwe monga ana mwa Yesu Khristu kwa iyemwini, malingana ndi—molingana ndi kufuna kwabwino kwa chifuniro chake.

132 Nanga bwanji izo, M'bale Mike? Kodi izo sizodabwitsa? Iye anakukondani inu. Iye anakukondani inu kusanakhale konse dziko. Iye ankachidziwa chikhalidwe chanu; Iye ankadziwa zifooko zanu; Iye ankadziwa zizolowezi zanu. Iye ankadziwa zonse za inu, chomwe inu mukanati mudzakhale. Ndiyene, pamene Iye anayang'ana kulikonse pa dziko lalikululi, monga izo zinaliri, Iye anati, "Ine ndikumuwona iye." Ndipo pamene Iye anachita izo, kusanakhale konse kachidutswa k—ka moyo, ndiye ndinu wamuyaya limodzi ndi Mulungu. Pamene inu mulandira Mzimu Woyera, ndiye inu mumakhala wamuyaya, chifukwa inu muli—inun munalali ndi Mulungu, ndinu gawo la Mulungu. Kodi inu mungakhoze kuona chimene ine ndikutanthauza? Ndinu wamuyaya limodzi ndi Mulungu, basi chifukwa inu muli. . .

133 Ine ndiri mochuluka basi Branham monga bambo anga anali Branham, chifukwa ndine magazi a Branham. Ndine Branham limodzi ndi bambo anga, chifukwa ine ndinabadwa kuchokera kwa abambo anga. Ndine Branham limodzi ndi iwo. Inu ndi Wood, chifukwa abambo anu dzina lawo ndi a Wood. Inu ndinu mochuluka kwambiri Wood monga Jim Wood aliri; ndinu basi Banks Wood. Amen! O, mai! Ndinu Neville chifukwa kuti bambo anu anali a Neville. Ndinu mochuluka basi Neville monga iwo analiri a Neville. Ulemerero! Ndiye basi amuyaya monga Mulungu aliri, chifukwa ndife gawo la Mulungu, ana aamuna ndi aakazi a Mulungu mwa Moyo Wamuyaya, ndipo sitingakhoze konse kuwonongeka. "Ine ndidzawaukitsa iwo mu masiku otsiriza."

134 Palibe zodabwitsa pamene iwo anakonzekera kuti adule mutu wa Paulo kumene kuja. . . Iye ankayenera kuti ayende njira ya imfa iyo. Iye analembera kalata yotsiriza ija kwa Timoteo, anati, "Ine ndamenya nkhondo yabwino; ine ndatsiriza ntchito yanga; ine ndasunga chikhulupiriro! Kuchokera pano waikidwira kwa ine korona yemwe Woweruza Wolungama ati adzandipatse ine pa tsiku ilo, osati ine ndekha, koma onse omwe amakonda kuwonekera Kwake."

Ndiye imfa inati, "Ine ndikukutsatira iwe."

Iye anati, "Mbola yako ili kuti?"

Manda anati, "Ine ndikupeza iwe."

135 Anati, "Kodi chigonjetso chako chiri kuti?" Koma iye anali ndi chitsanzo. Iye anayang'ana mmbuyo ku Kalvare ndipo anati, "Koma ndikuthokoza Mulungu yemwe amatipatsa ife

chigonjetso kupyolera mwa Ambuye Yesu Khristu.” Ndi inu apo. O, izo ziyenera kukondoweza zotengeketsa; izo ziyenera basi kuti zitero.

¹³⁶ Moyo uli...Mawu akupita kunja. Moyo, mawu a moyo amagwira Moyo, ndipo mkati mwa munthu wokhalapo chinachake chimayenera kufuulira kunja.

Inu mukudziwa, winawake anati, “Billy, nchiani chimawapangitsa anthu kudzuka apo ndi kuponyera mmwamba manja awo kapena kumati, ‘Ambuye alemekezeke!’ kapena ‘Ameni!’?” Penyani zomwe Baibulo limanena.

¹³⁷ Paulo anati, “Ngati ife tiyankhula mmalirime osadziwika, atani osaphunzira...Pamene iye wadalitsidwa—ngati iye wadalitsidwa, iye anganene bwanji, ‘Ameni?’” Mukuona? Iwe uyenera kuti uzidziwa chimene iwe kuchinena. Malirime osadziwika, kupatula ngati iwo ali mwa kutanthauzira kapena vumbulutso...Ndiye iwe ukhoza kunena, “Ameni!” ngati iwe ungakhoze kuzimvetsa izo. Iye akudziwa chomwe akuchinena. Mukuona?

¹³⁸ Tsopano! O, mai! Tayang’anani uko tsiku lija pamene mdani anali kubwera umo pa Davide. Ndipo iye anawapatsa iwo dende lonse la vinyo n—ndi—nthuli yabwino ya nyama ndi mkate. N—ndipo pamene mdani anali kubwera, iwo sanali kudziwa choti achite; ndipo iwo anasonkhana kumeneko; ndipo Israeli yense anasonkhana limodzi pansi pa mdulidwe. (Tsopano, izi zinali pansi pa mdulidwe wakale wa Chiyuda.) Ndipo iwo anakweza mmwamba manja awo ndipo anati, “Mulungu, Inu ndinu Mulungu wathu. Inu mwatiteteza ife. Inu munamubweretsa Mose mneneri, ndipo Inu munawabweretsa ana a Israeli kuchokera ku Igupto. Inu munawabweretsa iwo kudutsa mchipululu. Pamene iwo anali ali uko, palibe yemwe anachita mantha kuti—aliyense ankawopa kuti awakhudze iwo, palibe mmodzi anabwera pafupi ndi chuma Chanu. Iwo ankawopa kuti atero.” Komabe iwo anali apang’ono, koma aliyense ankawopa kuika manja ake pa iwo. Pakuti chirichonse chomwe chinkabwera pa iwo, iwo ankalumidwa mobwezera. Iye anati, “O, Inu ndi Mulungu wamkulu bwanji. Ndipo tsopano, Ambuye, ngati ife tachimwa...Akazi athu ndi awa; ana athu aang’ono ndi awa; ndipo ife tiri mu kusimidwa mu ora lino.” Anati, “O, kodi ife tingachite chiani? Mdani akubwera.” Iye anati, “Kodi ife tingachite chiani?”

¹³⁹ Ndipo pamene iwo anali kupemphera Mzimu unagwera pa mmodzi kumeneko mwa omvetsera, ndipo iye analosera, “PAKUTI ATERO AMBUYE, inu simumenyera; imani njii! (Ameni!) Pitani uko mwa njira *ina* ndi kukakomana nawo iwo kumeneko.” Ndipo Iye anayambitsa chisokonezeko pakati pawo, ndipo iwo anaphana wina ndi mzake. Ndi inu apo.

Kukonzedweratu kuti akhale osankhidwa mwa Khristu Yesu asanaikidwe maziko a dziko. Tsopano.

104. Inu munanena kuti munthu akhoza kumakhala moyo mwa pafupi kwambiri ndi Mulungu mwakuti iye sakanakhoza kuchimwa pamene iye ali pa dziko lapansi pano. Ndiye fotokozani I Yohane 1:8 mpaka 10.

¹⁴⁰ Tiyeni tiwone I Yohane 1:8 mpaka 10. Ngati ine ndikanakhala ndi kanthawi pang’ono kowonjezera kuti tiyang’ane pa izi...Ine ndinali nayo iyo; koma ine basi sindinaitenge iyo, amzanga. I—ine ndinali kuyesera k—kuti titulukemo...Chabwino, ine ndimupeza Yohane pakapita kanthawi. Ine ndi...Izo zikhala kumbali ina ya Ahebri, ndithudi. Chabwino. I Yohane 1:8 mpaka 10—I Yohane 1:8 mpaka 10.

Ngati ife titi...ife tiribe tchimo, ife timadzinyenga tokha, ndipo choonadi sichiri mwa ife.

Ngati ife tivomereza machimo athu, iye ndi wokhulupirika ndi wolungama kutikhulukira... machimo athu, ndi...kutitsuka ife ku kusalungama kwathu konse.

Ngati ife tinena kuti ife sitinachimwe, ife timupanga iye kukhala wabodza, ndipo mawu sali mwa ife.

¹⁴¹ Chabwino tsopano, dikirani m’bale wanga wokonedwa. Ingotembenezirani uko ku mutu wa 3 apa ndi ndime ya 9. Inu muli kumene pa tsamba lomwelo mu Baibulo langa. Ndime ya 8 kuti tiyambirepo:

Iye amene achita tchimo ndi wa mdierekezi; pakuti mdierekezi anachimwa kuchokera kuchiyambi. Pa cholinga icho Mwana wa Mulungu anawonetseredwa, kuti iye akakhoze kuwononga ntchito za mdierekezi. (Basi zomwe ine ndakhala ndikuziyankhula, mukuona, kukonzeratu kwa Mulungu, kukudziwani inu.)

Aliyense yemwe ali wobadwa wa Mulungu samachita tchimo; pakuti mbewu yake imakhalabe mwa iye: ndipo iye sangakhoze kuchimwa, chifukwa iye ali—iye ali—chifukwa iye ndi wobadwa wa Mulungu.

¹⁴² Basi ndi zomwe Mawu akunena. Tsopano, ngati inu mungapenye apa.

Ngati ife titi...ife sitinachimwepo, ife timupanga iye kukhala wabodza, ndipo mawu sali mwa ife.

Tsopano, anthu ena amati, “Chabwino tsopano, apa pali msungwana wamng’ono wabwino kapena mnyamata wabwino wamng’ono. Iwo sanayambe achimwapo pa kuyamba pomwe.” Inu munabadwa mu tchimo, munawumbidwa mu kusaeruzika, munabwera ku dziko kumadzanana mabodza. Pamene inu mubadwa mu dziko lino, ndinu wabodza, ndinu wakuba, ndinu

chirichonse chomwe chiripo, basi tchimo lonse, osati wakuba, chifukwa inu simunabepo. Koma ndinu—koma inu muli... Inu si wabodza, chifukwa inu simunayambe mwanapo. Koma mzimu umene uli mwa inuwo pamene inu mubadwa, chifukwa ndinu wa mdziko. Ndi chifukwa chake inu simungakhoze kukhala ndi kukonzedwanso, kukonzanso; inu muyenera kuti mufe ndi kubadwanso. Ndipo inu simungakhoze kukhala ndi kubadwa popanda kupachikidwa. Inu simungakhoze kukhala ndi chiukitsiro; inu muyenera kuti mupachikidwe kwa zinthu za mdziko ndi cholinga choti muukitsidwe mwa Khristu.

143 Ngati inu muti muzidalira pa k—kudziwa kwanu kwaluntha ndi zina zotero, inu simudzabadwa konse ndi Mzimu wa Mulungu. Inu muyenera kuti muziiwala, monga Paulo anachitira, zonse zomwe iye anayamba wazidziwapo, ndi kusadziwa kanthu pakati panu kupatula Khristu Yesu, ndi kubadwa mwatsopano, kachiwiri. O, ngati... Apa... Ngati ine ndingakhoze kuzifikitsa izo kwa inu. Mukuona? Ndi kubadwa komwe kumapangitsa chatsopano—cholengedwa chatsopano. Mawu omwe Achigriki apa, monga ine ndinali kuwayang'ana iwo mu Chigriki cha lexicon tsiku lina, mawu okuti *kubadwa* amatanthauza “chilengedwe.” Pamene iwo ati, “Inu muli—zolengedwa zatsopano mwa Khristu Yesu,” pali mawu apo, *cholengedwa* ndi mawu okuti *chilengedwe*. Inu ndi *chilengedwe* chatsopano, osati mu dziko, koma mwa Khristu Yesu. Inu mwakhala watsopano... .

144 Tsopano, inu munali mu dziko ndipo munkati, o, inu mukudziwa, zinthu zokopa, zovala zabwino kapena chokongola chinachake. Ndi...?...ziri kumbali. Mukuona? “O, ine ndimapita ku mpingo, zedi. Ine sindikufuna kuti ndidzapite ku gehena, koma inu mukudziwa...” Ndipo maso abulauni okongolawo kwa msungwanayo, kapena tsitsi laling'ono la mzindolo kwa mnyamatayo, kapena “Iye ali kwambiri...” Inu mukudziwa, chinachake kapena chinzake, chinachake basi choti chikope tcheru, kapena iye ndi wosilira kwambiri kapena—amamwa kapena chinachake kapena china apo. Ilo ndi dziko; inu m—inu muli mu dziko. Ndipo Baibulo linati, “Ngati inu mukonda dziko ndi zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri ngakhale mwa inu.” Chotero pofuna kuti muzichotse izo mwa inu, inu muyenera kuti mufe, muyenera kuti mufe, mupachikidwe, ndi kuikidwa mmanda, ndi kuukitsidwa cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu.

145 Tsopano, inu musanalandire Mzimu Woyera, inu mukukhulupirira kupita *ku* Moyo Wamuyaya. Koma inu mulibe Moyo Wamuyaya mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera, chifukwa Iwo ndi Moyo Wamuyaya. Mzimu Woyera ndi Mulungu; Ndi Moyo wa Mulungu mkati mwanu. Ndiye inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Kodi inu mukumvetsa izo tsopano? Mukuona? Penyani! Mukuona? Inu mukukhulupirira kupita *ku*.

146 Dikirani, apa pali chinthu chabwino. Akazi inu mundikhululukire ine chifukwa cha ichi ngati icho chitamveke mosabisa kwambiri (mukuona?)...tipange nsonga. Mayi amanyamula moyo...Komabe mwana uyo sanabadwe. Koma ngati inu muti mumusamalire mwana uyo molondola ndi kutsatira malangizo a chirengedwe, mwana ameneyo adzabadwa wolunga. Koma ngati inu simuyendetsa chirichonse monga mwa malangizo a chirengedwe, inu nkulola kachilonda kolimba, kapena kugunda, k—kapena chinachake kuchitika, i—icho—chimuwononga iye (mukuona?); icho chimupha mwanayo iye asanabadwe.

147 Chabwino, ndilo lomwe liri vuto. Zilonda zimabwera kuchokera kwa Satana. Satana amatenga zisonga za chiphe zaku gehena ndipo amayesera kuti awuvulaze nazo Mpingo womwe uli mu ululu wa kubadwa kwa mwana. Ndipo iye asanabadwe konse, iwo amamupha iye. Koma ngati inu mutangotenga Baibulo ndi kukadyetsa iko mu—kukapatsa iko chakudya cha mwana, amake kumadya mavitamini... Chabwino, iyi ndi Vitamini yopambana yomwe ine ndikuidziwapo, Mavitamini auzimu. Mukuona? Iwo amakumanga iwe.

148 Tsopano, mpingo ukuyenera kuti uzidya Mavitamini auzimu; ndipo Mavitaminiwo ali apa pomwe, Bukhu lonse lodzaza iwo. Ndipo inu muyenera kuti muzidya Mavitamini auzimu, kumaphunzira, ndipo izo zimabweretsa mwanayo ku kubadwa. Mukuona zomwe ine ndikutanthauza?

149 Tsopano, munthu wamng'onoyo, pamene i—i—iye ali ndi moyo—i—iye ali ndi moyo, chifukwa timaselo tating'onoto timasuntha ndi kumagunda pakangotha pafupi miyezi itatu ndi—kapena inai. Ndiyeno, iye amakankha ndi kumasuntha koma iye sanabadwe apabe. Koma mwamsanga iye akangobadwira mu dziko, adotolo, amake, kapena winawake, amamugwira apo iye ndipo [M'bale Branham akuwombetsa manja ake pamodzi—Mkonzi.] amamupatsa iye kumenya pang'ono, ndi “Ng'we-e-e!” A—apo iye amapita nazo (mukuona?), ndiyeno iye amayamba kupuma. Ndipo basi mwamsanga pamene iye apuma mpweya wa moyo, ndiye iye amakhala solo ya moyo.

150 Ndipo ndi chimene nthawizina... Inu mwakonzeka kuti mulandire Mzimu Woyera; inu muli mu ululu wa kubala; inu mukufuna kuti mubale. Ndi angati muno ali mu chikhaliidwe chimenecho pakali pano, akufuna ubatizo wa Mzimu Woyera, akufuna kwenikweni kuti adziwe chomwe izo ziri, akufuna kuti alowe—alowe mu izo? Nndani akufuna ubatizo wa Mzimu Woyera? Kwezani mmwamba manja anu. Mukuona? Inu muli mu kumvakuwawa, inu mukufuna—inu mukufuna kuti mubale. Chimene inu mukusowa ndi kumenya pang'ono kwa Uthenga, kenakake kakang'ono komwe [M'bale Branham akuwombetsa manja ake limodzi—Mkonzi.], ndipo inu mumafuulapo,

“Ulemerero!” Ndipo pamene izo zichitika. . . Ine ndikudziwa inu mukuganiza kuti ine ndapenga, koma i—ife tiri nawo malingaliro a Khristu omwe ali misala kwa dziko mulimonse. Chinachake chimakuwa mkatimu; Mzimu umenewo umatutuma. Ndiye Iwo umangopitiriza kubwera.

¹⁵¹ Monga ine ndinanena kwa munthu, ziri ngati mpope wakale umene unauma. Ndipo iwe umayendetsa kawayi kakang’ono kudutsa mmenemo, ndipo iwe umamugwira waya uyu ndipo iwe umakumba, kumba, ndi kukumba. Ndipo umo muli kuyenderera kwakukulu kwa madzi ukuyesera kuti adutsemo. Kukumba, kumba, kumba, iwe osakhoza kuwapeza iwo, koma iwe kumadziwa muli chinachake mmwamba umo. Iwe umakhoza kuwamverera iwo; iwo ali mmwambamo kumapeto uko. Ndiye pakapita kanthawi ukawapatsa iwo kukoka kwakukulu kwambiri, ndipo [M’bale Branham akusanzira phokoso la madzi amkokomo—Mkonzi.] amadutsa madziwo mu mpope. Umo ndi momwe izo ziriri. Ndiye madziwo amangopitirirabe kumabwera. Umo ndi momwe Mzimu Woyera uliri. Tchimo linaimitsa mapaiwiwo. I—inu mumakhala mmbuyomo nkumati, “Ndine wamanyazi. . .? . . . Inu mukudziwa. . .? . . . Ine ndikuchita mantha anthuwo aziganiza kuti ine ndinali. . . Mzimu Woyera.”

¹⁵² Tsopano, pamene inu mumverera kukoka kwakung’ono uko kwa Mzimu. . . Inu mumawufuna Iwo kuposa moyo—inu mumawufuna kuposa moyo wanu womwe. Iwo umatanthauza mochulukwa kwa inu: “Ine ndiyenera kuti ndikhale nawo Iwo kapena ndife.” Chinthu choyamba inu mukudziwa inu mumagwira chinachake. Inu mumaganiza, “Ndi chimenecho, Ambuye.” Inu mumachotsapo chitsekerocho. Psyfuuu! Apa iye amabwera! Zapita! O, mai! Mfulu! O! Mai! Pali. . .? . . . moyo tsopano umene ukukhazikika umo, ukuti. “Ulemerero kwa Mulungu. . .? . . .”

¹⁵³ Petro ndi iwo anali kuseri kuja pa Pentekoste akubisala, kumati, “Ziyang’ana panja pa chitseko mophweka kwenikweni, uziwona ngati aliyense wa Ayuda awo uko akubwera.”

“Ayi. Ine sindikumuwona mmodzi wa iwo.”

“Chabwino, khalani bata kwenikweni, chifukwa ine ndikukuuzani inu, ngati iwo ati abwere konse kuno. . .? . . .”

¹⁵⁴ Iwo anali onse atakhala apo, ndipo zonse mwadzidzidzi apo panadza mkokomo wochokera Kumwamba monga mphepo yamphamvu ya mkokomo. Iyo inayamba kudzaza nyumba yonseyo momwe iwo anali atakhala. Chinachake chinayamba kuchitika. Kuchokera mchipinda icho iwo anapita; anakankha natsegula zitseko, chotsika masitepe iwo anapita uko akudzandima ngati gulu la anthu oledzera pamene iwo anakhala ali. . .? . . . pa Mzimu, akungofuula ndi kumapitirira nazo.

155 Iwo anati, “Amuna awa aledzera. Tamvetserani pa iwo. Tayang’anani pa wamantha uja ankayang’ana pa chitseko, uja yemwe anamukana Yesu kumusi kuja pa kupachikidwa. Anati, ‘Ine sindimamudziwa nkomwe Iye.’ Mkazi wamng’ono anati, ‘Chabwino mayankhulidwe ako akukugwiritsa iwe. Ndiwe mmodzi wa iwo.” Anati, “Iye anatumwana, anati, ‘Ine sindikumudziwa Iye.’”

156 Koma pamene chitsekero icho chinasololedwapo, pamene Mzimu unayamba kuyenderera kudutsa mwa iye, iye anati, “Inu amuna amu Yudea, inu omwe mumakhala mu Yerusalemu, lolani ichi chidziwike kwa inu ndipo mveterani kwa ine. (Ameni!) Ndine bwanano. Lolani ichi chidziwike kwa inu; awa sanaledzere ayi. (Kuwuyankhulira mpingo wake.) Awa sanaledzere monga inu mukulingalira, powona kuti ili ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chiya chomwe chinanenedwa ndi mneneri Yoweli: ‘Zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse...’” U-nhu-u, kusiyana kwake! Psyfuu! Mai, ine ndikudziwa inu mukhoza kuganiza kuti ichi ndi chinthu chowopsya, koma i—i—ine ndiyenera ndikuloleni inu kuti muwone chomwe chiri Choonadi. Zikhalani ndi Icho.

157 Tsopano, ndithudi, inu muli nawo Moyo Wamuyaya.

158 Tsopano, kuti ndifotokoze izi. Tsiku lino . . . “Ngati ife tinena kuti sitinachimwe ayi (‘Tonse tachimwa ndipo taperewera ku ulemerero wa Mulungu’) ife timamupangitsa Mulungu kukhala wabodza.” Iye anati inu mwachimwa. Ngati inu munena kuti inu simunachimwe . . . Ine ndiri . . .

159 “Ine ndinabadwira mu mpingo wa Baptisti, mpingo wa Methodisti, mpingo wa Chipentekoste, mpingo wa Chipresbateria; ine ndinabadwira mmenemo.” Izo sizipanga kusiyana kochepe, inu muyenera kuti mubadwe kuchoka kwa izo kachiwiri. Ndiko kulondola. Ngati ife tinena kuti ife sitinachimwe, inu mukumupanga Iye kukhala wabodza. Ndipo Mawu, omwe ali Choonadi . . . Ndi angati akudziwa kuti Mawu ali Choonadi? “Pachiyambi panali Mawu . . . ndipo Mawu anasandulika thupi, ndipo Mawu . . .” “Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi. Mawu Anu ndiwo Choonadi.” Ndipo Iye anali Mawu. Mukuona? Ndipo Mawu, kapena Khristu sali mwa inu . . . Iye anali Mawu. Ndi angati akudziwa zimenezo? Mukuona? Chabwino.

160 Ife tiziwerenge izo monga chonchi ndiye: “Ngati inu munena kuti inu simunachimwe ayi, inu mukumupanga Iye kukhala wabodza ndipo Khristu sali mwa ife.” Mwaona, mukuona? Tsopano, ndizo . . . Mwaona, pamene inu munena kuti muli—kuti inu simunachimwe, inu mukulakwitsa. Inu muyenera kuti mubadwe kachiwiri.

161 Tsopano, ife titembenuzira uku pa ndime ina iyi. “Iye... Aliyense yemwe ali wobadwa wa Mulungu samachita tchimo, samachita tchimo, pakuti...”

162 Tsopano kodi tchimo ndi chiani? Ndani wanena izo, winawake? Kusakhulupirira. Ndi chomwe Baibulo linanena. Pali tchimo limodzi lokha, ndipo ndilo kusakhulupirira. Ndiko kulondola. “Iye amene sakhulupirira ali woweruzidwa kale.” Koteru inu—wina achimwa.

163 Tsopano, ngati inu mukuti, “Chabwino tsopano, dikirani miniti. Ine ndikukhulupirira kuti iwo ayenera kuti ankalandira Mzimu Woyera monga chomwecho mu masiku amenewo, koma ine sindikukhulupirira kuti ziri chomwecho.”

164 “Koma, m’bale, Baibulo linati, ‘Lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu.’”

“Ine ndikudziwa, koma...” Inu mukuchimwa. Inu mukuchimwa apo pomwe. Inu simukukhulupirira zomwe Mulungu ananena.

“Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

165 “Chabwino tsopano, tinaphunzitsidwa kuti...” Ine sindikusamala zomwe inu munaphunzitsidwa. Baibulo linati— Iye anati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza ndipo Anga akhale owona.” Chabwino.

Inu mukuti, “Chabwino, Iye—mwamfundo Iye ali yemweyo, koma ine sindiri... Inu mukutanthauza kuti Iye ali yemweyo?”

“Eya, mu Mpingo akuchita zinthu zomwezo zimene Iye ankachita pamene Iye anali kuno.”

166 “O, ine sindingakhoze kukhulupirira izo.” Inu mukuchimwa. Inu mukuchimwa. Ndipo iye yemwe ali wobadwa wa Mulungu, wa Mzimu Woyera, samanena zinthu zimenezo. Ndipo ngati iye anena kuti ali nawo Mzimu Woyera ndi kumanena zinthu zimenezo, uwo ndi umboni woti iye alibe Iwo. Ine sindikusamala zomwe iye wachita. Ngati iye sakukhulupirira mu machiritso Auzimu, samakhulupirira mu Mphamvu ya chiukitsiro, samakhulupirira mwa Mzimu Woyera kuti ukutsanuliridwa pa ife ndendende basi monga Iwo unachitira mu m’badwo woyamba, Mulungu yemweyo basi dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, zinthu zomwezo zimene atumwi anachita zikuchitika pakali pano, kuyankhula mu malirime, ndi kusangalala, ndi zinthu zina zonse izi; ngati iwo samakhulupirira izo, iye sanabadwe wa Mulungu. Pakuti aliyense yemwe ali wobadwa wa Mulungu samachita za mtundu umenewo. Ndi momwe mungadziwire ngati iwo anabadwa a Mulungu.

167 Inu mutapita kwa munthu ndi kukati, “Dr. Ph. *Wakuti-n-wakuti-n-wakuti*, M’busa, Dr., kapena *Wakuti-n-wakuti* (zomwe ziri zabwino, ndikukhumba ine ndikanakhala

nazo izo, digirii'yo), koma kodi izo ziri chomwecho kuti machiritso Auzimu azichitidwa mu mpingo basi monga atumwi ankachitira?"

"O ayi, ayi!" Iye akuchimwa. Iye ndi wosakhulupirira. Uko nkulondola.

¹⁶⁸ Inu mukati, "Kodi inu mukukhulupirira kuti ife timalandira Mzimu Woyera monga iwo ankachitira apa? Ine ndinali kuwerenga apa mu Baibulo ku Machitidwe 2 pamene Ilo linanena kuti iwo anali...ndipo ankatsanulira apo Mzimu Woyera, ndipo iwo anadzandima ngati kuti iwo anali ataledzera, ndipo iwo anapita uko ndi kumayankhula mu zinenero za anthu amenewo, ndi zinthu monga chomwecho; ankachita monga anthu omwe anali ataledzera, ndipo mpingo ukaganiza kuti iwo anali ataledzera. Pamene ife tilandira Mzimu Woyera lero mu mpingo wa Baptisti, Baptisti yathu, Methodististi yathu, Presbateria yathu, chirichonse chomwe chingakhoze kukhala chiri, i—ine sindikuwona ife tikuchita izo."

"Chabwino, ine ndikukuuza iwe, mwananga, izo zinali za khumi ndi awiri okha aja." Iye akuchimwa. Iye sanabadwe mwa Mzimu wa Mulungu, chifukwa Baibulo linati, "Iye amene ali wobadwa mwa Mzimu wa Mulungu samachita kusakhulupirira. Iye ndi wokhulupirira, ndipo iye sangakhoze..." Bwanji? Bwanji? O, apa izo ziri. Nkhunda ili mkati mwake, ikumutsogolera iye. Pakuti Mzimu wa Mulungu uli mkati mwa iye, ndipo iye sangakhoze kuwukana Iwo; iye sangathe. Ngati iwo uli Mzimu wa Mulungu, Mulungu sangawakane Mawu Ake omwe. Ngati ine ndingawakane mawu anga omwe, ndiye ine ndimakhala wabodza. Ndipo n—ndipo ngati inu mukuti inu muli nawo Mzimu wa Mulungu ndi kumawakana Mawu a Mulungu, mwina Mulungu ndi wabodza kapena ndi iweyo wabodza, china kapena chimzake. Ndipo Baibulo linati, "Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza ndipo Anga akhale Choonadi." Ndipo munthu yemwe wabadwa ndi Mzimu wa Mulungu sangakhoze kutsutsana ndi Mawu a Mulungu; iye ayenera kumanena kuti Iwo ndi—olondola. Iye sangakhoze kuchita china chirichonse. Mvetserani, ichi ndi Choonadi.

¹⁶⁹ Mvetserani, ndiroleni ine ndiwerenge izi kachiwiri.

Aliyense yemwe wabadwa wa Mulungu samachita tchimo; pakuti mbewu...

¹⁷⁰ Kodi mbewu ya Mulungu ndi chiani? Lonjezo kwa Abrahamu—analisi ndi mbewu kwa...Kodi mbewu ndi chiani tsopano? Khristu. Kodi Khristu ndi Mbewu ya Mulungu? Ndi Mbewu ya ndani Iye ngati Iye asali? Chabwino, chabwino. Iye ndi Mbewu ya Mulungu.

¹⁷¹ Mbewu ya Mulungu imakhalabe ili mwa iye. Mzimu Woyera umabwera kudzakhalamo, osati kuchokera ku msonkhano kupita ku msonkhano, koma kwa muyaya. Tsopano, ngati

inu mukufuna kuti mulembe izo, Lemba lanu la izi, Aefeso 4:30: “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Mbewu ya Mulungu imakhalabe ili mwa iye, ndipo iye sangakhoze kuchimwa, chifukwa iye ndi wobadwa wa Mulungu. Iye sangakhoze kusawakhulupirira Mawu a Mulungu.

¹⁷² Tsopano, pamene inu mumuwona munthu asakugwirizana nawo Mawu a Mulungu ndi kumati, “O, izo zinali za m’badwo wina,” pamene lonjezo liri kwa aliyense yemwe afuna muloleni iye adze, ingokumbukirani, iye ndi wosakhulupirira ndipo iye si wa Mulungu.

Ife kuli bwino tiimire apa, sichoncho ife? Kodi ndi nthawi yanji? O, mai! Ine ndiri—i—ine basi—ine sindikufuna kuti ndidzabwerenso kuno Lamlungu. Ndiloleni ine ndingotenga izi mwaliwiro kwenikweni, kwenikweni basi. Ndingatero ine? Ndi zabwino kwambiri basi. Kodi inu simukuganiza kuti ndi zabwino? O, Mawu a Mulungu. Chabwino.

M’bale Branham, kodi munthu azichita chiani...

Ndiroleni ine ndigwirizire izo kotsiriza, nditenge izi apa.

105. Kodi ndi mawonekedwe anji omwe ife titi tidzakhale tiri mu chiukitsiro?

¹⁷³ Momwe ife tinaliri pamene ife tinkapita pansi. Ndendende, chiukitsiro... Basi—tangoganizani za izi. Bukhu ili likagwera pansi [M’bale Branham akugwetsa bukhu—Mkonzi.], ndipo ine ndikalitola bukhu ili, bukhu losiyana, ndi kuliika mmalo mwa ilo. Ichu si chiukitsiro. *Chiukitsiro* ndi “kudzutsa chomwecho chimene chinapita pansi.” Kodi Yesu anaukitsidwa? Kodi iwo ankamudziwa Iye? Kodi Iye anali kuima ndi iwo, Yesu yemweyo? “Ndipo Yesu yemweyo yemwe anatengedwera mmwamba, adzabwerenso mu mawonekedwe ofanana monga inu mukumuwonera Iye akupita.” Chiukitsiro chiri basi ngati pamene inu mufa; umo ndi momwe inu muti mudzawukire. Inu mumafa ngati munthu mu mnofu; inu mudzawuka ngati munthu mu mnofu. Ndizo basi ndendende. Chotero chiukitsiro chiri basi mofanana. Ife tikhoza kutha maora ena awiri pa izo, koma ndi bwinoko kuti ife tisaziyanbe.

106. Tafotokozani Ahebri 4 ndi 6 (Mofulumira ndithu tsopano, ife tizitenge izi mofulumira ndithu.) ndipo fanizitsani apo ndi Ahebri 10:26—Ahebri 6 ndi 4. (Ine ndikupempha kukhululukira kwanu, 6:4, ndi 10:26. Tiyeni tiwone, 10:26; chabwino, ine ndiri nazo izo apa pomwe. Mukuona?)

Pakuti ndi kosatheka kwa iwo omwe nthawiyina anaunikiridwapo, ndipo atalawapo... mphatso zakumwamba, ndipo anapangidwa kukhala olawa nawo za Mzimu Woyera,

Ndipo pokhala atalawa mawu abwino a Mulungu, ndi mphamvu za dziko likudza,

Ngati iwo angati agwe...kuti adzikonzenso iwoeni kachiwiri mwa kulapa; powona kuti iwo adzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu katsopano,...ndipo amuika iye ku manyazi apoyera.

174 Izo zikupita patsogolo ndithu ndi kunena zomwe izo... Tsopano penyani. Ine ndinali nazo izo usiku wina. Ndi angati anali muno pamene ine ndinkazifotokoza izo? Chabwino, inu mukudziwa chomwe izo ziri apo. Onani, ndi okhulupirira a mmalire awo.

175 Ndi angati anawerenganso mu Deuteronome 1 umo, pamene azondi anapita umo momwe ndipo analawa zinthu za mu Kenani, chomwe Kenani si choimira Zakachikwi. Ndi angati akudziwa zimenezo? Inu mukutanthauza, dzanja limodzi lokha? Junie. Uko nkulondola. Kenani si choimira Zakachikwi, chifukwa iwo anali ndi nkondo, kumenyana, kuphana, ndi china chirichonse mu Kenani. Kuimira Woyera—Kenani ndi choimira Mzimu Woyera. Igupto ndi dziko lomwe iwo anatulukamo. Chipululu ndi komwe iwo anayeretsedwako, Mpingo woitanidwa kuti atuluke. Kenani ndi komwe iwo anakhazikikako ndi Mzimu Woyera (mwaona, mukuona?), chifukwa iwo anali nazobe nkondo. Ndipo ngati inu simukhulupirira kuti muli nazo nkondo, mudzangolandira Mzimu Woyera kamodzi.

176 Kodi inu mukuchita chiani? Kodi iwo ankachita chiani mu Kenani? Iwo anali kutenga mafulu awo. Ulemerero! Iwo anali kutenga mafulu awo. Ndipo iwo sakanatenga mafulu awo mpaka iwo atafika mu Kenani. Iwo analibe kanthu kalikonse mu chipululu. Ndiye, pamene iwo anabwera mu Kenani, ndiye iwo anali nawo mafulu. Ndipo ife tiri nawo mafulu. Pamene inu mulandira Mzimu Woyera, inu muli mu Kenani. Inu muyenera kuti muzimenyera iwo; inchi iliyonse ya nthaka inu muyenera kuti muzimenyera iyo. Inde, bwana! Ndicho chifukwa anthu amati, “M’bale Branham, inu mundipempherere ine lero.” Kafikeni mu Kenani umo kamodzi, m’bale, ndipo inu mumazindikira komwe kuli kwanu. Penyani pemphero likuyamba...?...Inde, bwana!

Iye anati, “Penya kuno, Satana. Ili ndi langa! Ndine mwini wa ili! Mulungu ananena chomwecho! Suntha nuchoke! (Ndiko kulondola!) Suntha chokapo pa malo anga!”

“Malo ako?” Satana amatero.

“Ine ndiri nawo umwini wamtheradi kwa iwo. Suntha nuchoke! Mawa ine ndipereka chenjezo pa iwe mwa utsogoleri wa Mzimu Woyera.” Iye amasuntha nachokapo. Zedi, iye ayenera kutero.

177 Tsopano, tsopano, iwo amene analawapo mphatso ya kumwamba...Tsopano, penyani cha apa.

...ngati ife tichimwa mwadala... (ya 10, iyi ndi ya 26 ya mutu wa 10.)...ngati ife tichimwa mwadala titatha... ife titalandira kale chidziwitso cha choonadi, apo sipakhalanso nsembe yina kwa machimo,

178 Tsopano, chimodzi cha izo ndi pamene inu mwangolawa kumene za izo, ndipo chotsatiracho ndi pamene inu mwalandira ndipo mwapeza chidziwitso cha izo. Ndiye ngati inu muchimwa motani? Kusakhulupirira... Tsopano, penyani momwe zonsezo zikuwerengekera. Mukuona? “Ngati inu muchita kusakhulupirira mwadala mutalandira kale chidziwitso cha choonadi...” Tsopano lolani... Miniti yokha, munirole ine ndizitenge izi apa.

Ngati ife titi tidzagwe, kuti tidzikonzenso tokha...

...ndi kosatheka kwa iwo omwe nthawiyina anawalitsidwapo, ndipo analawapo za mphatso zabwino zakumwamba... (Analawapo za izo. Mukuona?)... ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo... (Mukuona?)... za Mzimu Woyera.

Ndipo analawapo za mawu abwino a Mulungu, ndi... mphamvu za dziko likudza,

179 Ndipo iye akupitirira mpaka pansu apa ndi kunena kuti ngati inu munangokhala ngati nansongole, pamene mvula imabwera pa dziko lapansi; ngati inu mumangokhala ngati nansongole, Mzimu Woyera utagwa, ndipo o mai, inu munamva kukoma Iwo mochulukha basi monga ena onsewo; koma kunena za kuika manja anu pa Iwo ndi kumapita kunja uko, kukawagwirira ntchito Ambuye, ndi kumachita chinachake pa izo, ayi, ayi, inu simungakhoze kuchita izo. Mwaona? Ndiye izo zimasonyeza kuti Mzimu wa Mulungu sulii mwa inu. Mukuona? Ndiye inu basi potsiriza mumangodzimangiriza nokha. “Zomwe mapeto ake ndi kuti zidzawotchedwe.”

180 Koma cha apa, ngati ife sitikhulupirira... Tsopano, kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira. Ngati chinthucho chadziwitsidwa kwa inu, ndipo inu nkutembenuka nkuchoka kwa icho mwadala ndi kuti, “I—i—ine sindikufuna kanthu koti ndichite,” inu mutachiwona kale icho, icho sichidzaitana konse kwa mtima wanu kachiwiri. Inu mwatha; ndiko kulondola. Inu muli—inu mwachimwa nkulichotsa tsiku lanu la chisomo. Mukuona?

Pakuti ngati ife tichita kusakhulupirira mwadala... (Tsopano, mu Baibulo langa ine ndinazisonyeza izo apa pamene izo ziri... Pali “m,” kuwerenga kwa mmphepete apa, akuti: tchimo—kusakhulupirira mwadala. Mwaona, mukuona?)...mwadala kale... ife titalandira kale chidziwitso cha choonadi, apo sipatsalanso nsembe yina kwa tchimo ilo, (Ngati inu muchokapo ndi kumukana Mulungu mwadala zonsezo

zitapangidwa bwino bwino kwa inu, ndi Mulungu atazipereka izo kwa inu. . . Mukuona?)

Koma kuonekera kwina kowopsya kwa chiweruzo cha ukali wamoto, womwe uti udzamalikhwire mdani.

Iye yemwe ankanyozetsa lamulo la Mose ankafa popanda chifundo pansi pa mboni ziwiri kapena zitatu:

. . . ndi chilango chinanso chochuluka bwanji, chomwe mukulingalira chikuyenera inu, kuti chidzakhala. . . chidzakhale ngakhale chiri choyenera, omwe mwapondereza pansi pa phazi Mwana wa Mulungu, ndipo mwayesa. . . phangano, lomwe iye anayeretsedwa nalo, chinthu chosayera, ndipo. . . munachita mosasamala kwa ntchito za chisomo? (O, mai!)

¹⁸¹ Kodi zikanakhala chiani? Mlaliki, mtumiki, tiyeni tingotenga. . . Chifukwa ine ndine mlaliki, tiyeni timutenge mlaliki. Amakwera pano, kubwera apa, kudzinenera za Khristu, ndi kufika kumene pamene inu simumakhalanso mu zigololo ndi zinthu aponso, kumakhala moyo wabwino woyera, kumabwera pano; chisomo cha Mulungu chitakhala chiri chabwino kwa iye, ndiye iye amayenda mpaka mu chidziwitso cha Mzimu Woyera momwe (mukuona?), amayenda mpaka apo, Mulungu akumutsogolera iye mpaka apo pa chidziwitso cha Mzimu Woyera, ndipo apo iye amawuwona Iwo, koma iye amati, “Tsopano, dikirani miniti. Mpingo wanga sungaime ndi zimenezo. Ine sindingakhoze kuchita izo. Iwo angandithamangitsire ine kunja. K—khonsolo ingandithamangitsire ine panja. Msonkhano wotsatira wa atumiki, ine ndingachotsedwe.” Apo sipamakhala nsembe inanso kwa tchimolo, chifukwa iye watenga Magazi awo omwe amene anamuyeretsa iye ndipo amubweretsa iye mpaka apa, ku chidziwitso cha Choonadi, ndipo wachiyesa Icho ngati kuti Icho chinali chinthu chosayenera ndipo wachipondereza Icho pansi pa mapazi ake, Mulungu atamutsogolera kale iye phazi ndi phazi kukwera apa kwa Mzimu Woyera.

¹⁸² Inu mukuti, “O, tsopano dikirani miniti, M’bale Branham.” Miniti yokha! Mzimu wa wotsutsakhristu ungachite izo. Kodi inu munazindikira mitu iwiri ya iwo? Kodi Yudasi Iskarioti anali ndani? Mdierekezi! Baibulo linati iye anali mwana wa chiwonongeko. Kodi chiwonongeko ndi chiani? Hade. Iye ndi mwana wa hade, anachokera ku hade ndipo anapita ku hade. Ndipo Yesu Khristu anali Mwana wa Mulungu, anabwera kuchokera Kumwamba, anabwerera Kumwamba. Pamene onsewo anafa p—pa mitanda. . . Yudasi. . . Kodi inu mukudziwa kuti Yudasi anafa pa mtanda? Ndi angati akudziwa zimenezo? Iye anafera pa mtengo. Yesu anafera pa mtengo nayenso. Iwo unachita kudulidwa; ndizo zonse. “Wotembereredwa ali iye

yemwe aferu pa mtengo.” Ndipo iye anabwera kuchokera ku gehena. Ndipo tapenyani zomwe...Utali wonse momwe iye anapezera njira yake yolowera mu mpingo...Ndiwo utali womwe iye angakhoze kubwera tsopano. Mukuona momwe iye angakhoze kukhalira wachinyengo, momwe Yudasu amadzera? Kodi iye anali chiani? Msungichuma, m'bale, akugwira ntchito mu mpingo, msungichuma mu mpingo anakhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo anali basi monga...[Tepi itha mosatsirizitsa—Mkonzi.]



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org